# *Ululu Wa Kubala*

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

2 Wokondedwa Mulungu, ndife othokoza kwambiri lero chifukwa cha kutsanulira kwakukulu kwa Kukhalapo Kwanu, pakati pathu, kale. Ndipo ife tikuyembekezera izi, mopitirira, mochuluka, madzulo ano. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha nyimbo yopambana iyi yochokera kwa mkazi wabwino wa Chikhristu uyu amene wangoyimba nyimbo iyi; ndi Mzimu Wanu umene unatsika, ndi kutanthauzira kwake. Ambuye, mulole izo zikhale chomwecho, ife tikupemphera. Ndipo, Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mudalitse aliyense wa ife, ndipo mulole mitima yathu idzadzidwe ndi chisangalalo pamene ife tikuziwona izi zikuchitika.

3 Wokondedwa Mulungu, ife tikupemphera, madzulo ano, ngati pali ena pano amene sanakonzekere kuti akomane ndi Inu, mulole ili likhale ora limene iwo ati apange lingaliro lotsiriza limenelo ndipo abwere mwa Inu, kudzera mu Kubadwa kwatsopano. Perekani izi.

4 Tidalitseni ife tonse, Ambuye, amene takhala nthawi yayitali panjira. Ife tikupemphera kuti Inu mutiphunzitse ife zinthu zatsopano mwa Mawu Anu. Tipatseni ife kumvetsa kwabwinoko mwa Mzimu Wanu, Ambuye. Mulole Iye abwere ndipo adzatanthauzire Mawu. Wotanthauzira yekhayo amene tiri naye ndi Mzimu. Ife tikupemphera kuti Iye apereke izo kwa ife, lero. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

5 [Mlongo akuyamba kunenera. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Zimenezo zikukwanira. Ndi nthawi yotani! Ine sindikudziwa malo abwinoko oti ndikhaleko, pokhapokha kutakhala Kumwamba, pakuti ife tikungomverera kudzoza kwa Iko tsopano, mwaona, titakhala limodzi mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, titasonkhana mmalo Ammwambamwamba.

6 Mulungu amudalitse Mlongo Florence! Ndipo iye akudutsa mu nthawi yachisoni, ndi mithunzi; abambo ake angotengedwa kumene. Ndipo ine—ine ndikupemphera, "Mulungu, mudalitseni mwana ameneyo."

7 Ndipo M'bale Demos, atanyamula pa mapewa awiri onse, ndi kulemera kwa misonkhano yayikulu yonseyi ndi zinthu. Iye akusowa mapemphero athu, nayenso. Mulungu amudalitse M'bale Shakarian!

8 M'bale Carl Williams, ndine wokondwa ndithudi kukhala pano mu msonkhano waukulu uno ndi inu, pakati pa abale onse abwino awa. Ndipo ine ndinali ndi mwayi wokumana

ndi ena. Ndipo tsopano ili ndi gawo langa lomaliza la utumiki, monga momwe ine ndikudziwira, chotero, bwanji, ine ndikuyembekeza tsopano kuti ndikhoza kugwirana chanza ndi ena a amuna abwino awa, ndi—ndi kukumana nawo, pakuti ndikuyembekezera kukakhala Muyaya ndi iwo, mu—mu Dziko labwinolo.

9 Basi—chinthu chaching'ono, ine ndikuyembekeza ine sikuti sindimvetsedwa. Ndipo osati mwangozi, ine sindikuganiza, chifukwa ine—ine ndikuganiza kuti izo zinali zoperekedwa, kuti dzulo ndinapatsidwa mphatso ndi mzanga kuno, yochokera kwa mzanga wa ine, Danny Henry. Iye anali mnyamata . . . Tsiku lina, mu msonkhano wa a Christian Business Men mu California, ine ndinali ndi—msonkhano. Ine ndinali kuyankhula molimba kwambiri motsutsa—chikhalidwe cha nthawiyo.

10 Ndipo ine—ine ndikuyembekeza kuti aliyense akumvetsa zimenezo, osati kuti ndiri ndi choipa mu mtima mwanga. Si zimenezo ayi. Ayi. Inu ndithudi mumvetsa kuti sindikutanthauza izo mwanjira imeneyo. Koma ine ndikungoyenera kunena chimene chabwera kwa ine kuti ndinene.

11 Ndiyeno zikatha zimenezo, mwamuna wamng'ono uyu, m'bale wa Baptisti . . . Ndipo ine ndikuganiza kuti ndi wachibale wina wa katswiri wa pakanema. Ndipo anabwera kuti adzayike dzanja lake mondikumbatira ine, ndi kudzati, "Ambuye akudalitseni inu, M'bale Branham. Ine ndikungofuna kuti ndipemphere." Ndipo iye anayamba kuyankhula mu Chifaransa. Ndipo mnyamatayo samadziwa liwu limodzi la Chifaransa.

12 Ndipo winawake anadzuka, wokhala ngati mkazi wamkulu. Wochokera . . . Ine ndikukhulupirira iye anali wochokera ku Louisiana. Iye anati, "Chimenecho ndi Chifaransa."

Ndiye panali mwamuna pamenepo, anati, "Chimenecho ndi Chifaransa."

13 Ndipo iwo anali atalemba chimene icho chinali. Ine ndiri ndi zolemba zoyambirira apa. Ndiyeno, zinachitika kuti, mnyamata wamng'ono akuyenda kuchokera kumbuyo, ndipo akubwera kutsogolo, ankafuna kuti awone zolemba zawo. Ndipo iye anali wotanthauzira Chifaransa wa UN. "Ndendende basi Chifaransa."

14 Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge cholemba ichi. Ichi ndi cholembedwa chapachiyambi cha mmodzi wa iwo, ndipo chinali chochokera kwa munthu uyu amene anamasulira, sindingathe kutchula dzina lake molondola, Le Doux, Victor Le Doux, iye ndi wamagazi Achifaransa kwathunthu. Tsopano, uthengawo ndi uwu:

*Chifukwa iwe wasankha njira yopapatiza, njira yolimba, iwe wayenda mwa kusankha kwako komwe, iwe watenga*

*lingaliro lowona ndi lolondola, ndipo imeneyo ndi NJIRA YANGA.*

*Chifukwa cha chisankho chofunikira ichi, gawo lalikulu la Kumwamba likukuyembekezera iwe. Ndi lingaliro laulemelero bwanji limene iwe wapanga!*

*Ichi, mwa icho chokha, ndi chimene chidzapereke, ndi kudzakwaniritsa, chigonjetso chopambana mu Chikondi Chaumulungu.*

15 Pamene ine ndinapeza icho. . . Inu mukudziwa, pamene ine ndinamva koyamba anthu akuyankhula mmalirime, ine—ine sindinadzudzule kalikonse, mwaona, chifukwa ine ndaziwona izo ziri zenizeni, koma, nthawizonse ndinkadabwa. Koma pamene izo zinadzachitika, ndipo podziwa chimene ntchitoyo inali, kuseri kwake, ine—ine ndinadziwa kuti izo zinachokera kwa Mulungu.

16 Kenako, m'bale wake wakhala apa, a—woyimira mlandu weniweni wodziwika, anandipatsa ine mphatso yochokera kwa Danny. Danny wangochoka kumene ku Dziko Loyera. Ndipo iye anakagona pa manda, mmanda, kani, pamene Yesu anayikidwa itachitika imfa Yake. Ndipo pamene iye anatero, iye anati anayamba kundiganizira ine. Ndipo—ndipo Mzimu wa Ambuye unadza pa iye, ndipo iye anapita pa Phiri la Kalvare kumene kupachikidwa kunachitika, ndipo anatenga chidutswa cha mwala. Ndipo anabwererako ndipo anandipangira ine zomangira mikono ya malaya kuchokera mwa iwo. Ndipo ndimazikonda izo kwenikweni.

17 Ndipo tsopano, ichi, ndithudi, Danny sakudziwa zimenezi. Koma, mmawa uno, pamene ndinali uko mu pemphero, ine ndinangoyang'ana pansi pa zomangira mikono ya malaya zimenezo, ndipo chirichonse cha izo, ngati mungazindikire, chiri ndi madontho a magazi, komanso chiri ndi mzere wowongoka pa chirichonse. Ndipo apa mu uthenga umene iye anawupereka wochokera kwa Mulungu, wa njira yowongoka, yopapatiza. Momwe izo zinangokwanira, chimodzimodzi basi! Ine ndinaganiza kuti izo mwinamwake zinali zongoperekedwa kapena. . . Ndipo ine ndithudi ndikumuthokoza Danny. Inu mukamuuze iye, m'bale, momwe ine ndikuyamikirira izo. Ndipo chachi-. . . Chinthu china chachirendo, ndinamufunsa mkazi wanga m'mawa umene ine ndinavala malayawo, ndimayenera kuyika zomangira mikono ya malaya mmenemo, ndipo iye anati, "Ine ndinaiwala kukubweretsera zomangira mikono ya malaya zako," chotero Ambuye anali atandipatsa zina.

18 Oh, ndi moyo waulemelero! Sichoncho inu, abale? Kungoyenda mu kuphweka kwa—kwa Uthenga! Ndipo komabe, mu kuphweka Kwake, Iwo ndi chinthu chachikulu kwambiri chimene ine ndikuchidziwa. Ine sindikudziwa kanthu za Iwo. Ndipo pokhala kuti Iwo unapangidwa mophweka, kuti ine

ndinali ndi mwayi wobwera mwa Iwo, mwaona, nanenso, mwa chisomo cha Mulungu.

19 Tsopano, madzulo ano, ine sindikufuna kuti nditenge nthawi yochuluka, chifukwa ine ndikudziwa inu mukupita ku matchalitchi usikuuno. Ine ndikuganiza, alendo nonsenu pano mukuyenera kuyang'ana mozungulira pa nsanja, muwaone atumiki awa, ndipo iwo ali, oh, iwo akakhala okondwa kukhala nanu mu utumiki wawo usikuuno. Iwo akakuchitirani inu zabwino. Sindikukayikira inu munapita ku Sande sukulu ina mmawa uno mu mzinda. Ndipo pamene ife tikukhala ndi misonkhano yayikulu iyi, ndipo pokhala a Full Gospel Business Men, ine ndikuganiza kuti tikuyenera kupereka chithandizo chathu chonse chimene ife tingathe ku mipingo yathu, chifukwa kumeneko ndi kumene amuna amalonda athu amapita. Ndipo, tsopano, iyo ndi nyumba ya Mulungu, ndipo ine ndikuyembekeza inu muyendera tchalitchi china usikuuno.

20 Mawa usiku ndi kutsekera kwa msonkhano waukulu, ine ndikukhulupirira, ndipo ine ndikuganiza iwo alengeza wodzayankhula. Chimene, ine ndikulinga zodzakhala kuno, Ambuye akalola, kuti ndidzamve uthenga wake.

Mulungu adalitse wina aliyense wa inu.

21 Tsopano, ine ndiri, sindimadzinenera kuti ndine mlaliki. Ndine—ndine wokhala ngati...Ine ndiribe maphunziro okwanira kuti ndidzitche ndekha mlaliki. Mlaliki, mukanena zimenezo, iwo amayembekezera kuti ukhale ndi madigrii angapo ku koleji. Ndipo—ndipo ine ndiribe kalikonse koma legeni yaying'ono *Iyi*. Mukuona? Ine ndimayesetsa kutsatira nkhosa zodwala, ngati ine ndingathe, kuti ndizibwezeretse ku msipu wa Atate.

22 Ngati ndilakwitsa, mundikhululukire ine. Sindine wa fioloje. Ine sindimatsutsa a fioloje. Fiolo-...Fioloje ndi yabwino. Ndi zomwe ife timazifuna. Koma nthawizina ine ndimadzudzula chikhalidwe chimene ife talowamo. Izo sizitanthauza kwa munthu winawake. Ndi Uthenga basi. Ine—ine ndikanakonda kuti Iwo usakhale wanga kuti ndiwupereke. Izo zimandikhadzulira ine mzidutswa, chifukwa iwe umadziwa momwe umamverera ndi ana ako omwe. Mukuona? Kodi inu simudana nazo kuti muzimudzudzula mwana, kumulalatira, kapena chinachake, ngakhalebe? Ndine kholo, nanenso, ndipo ndikudziwa chimene izo zimatanthauza. Ndipo ine—ine ndikudalira kuti inu mundikhululukira ine.

23 Ndipo ine ndikufuna kuti inu muchite monga chonchi. Pamene inu mwakhala, madzulo ano, ndikufunsani inu kuti mundikonde. Ndangokhala ndi zolemba zazifupi pang'ono, zapang'ono apa. Monga ine ndakuuzani inu, ine ndikuyenera kuti ndipange izi, ndilembe Malemba anga. Kale, ndinkatha pafupifupi kutchula za mu Baibulo pamtima, koma osati

tsopano. Ndadutsa mu nkhondo zolimba zambiri, ndakalamba kwambiri kuti ndizichita zimenezo. Koma ine ndikudalira kuti—kuti mundimvetsera ine kanthawi pang'ono, madzulo ano, ndipo mungotsegula kwenikweni mtima wanu ndi kuyesetsa kumvetsetsa zimene ndikuzifukula. Ndiye ine ndikuganiza izo zikhala bwinoko, makamaka azibusa a mzindawu ndi malo osiyanasiyana. Ine—ine ndikudalira kuti mumvetsera mwatcheru kwenikweni.

24 Ndipo tsopano muchite zimenezo, muzichita zimenezo momwe ine ndimachitira pamene ine ndikudya chitumbuwa changa chokondedwa, cha nthudza. Ina ya nyama imene ndimaikonda, nkhuku. Koma pamene ndikudya chidutswa chabwino cha chitumbuwa cha nthudza ndipo ndikapeza njere, ine sindimasiya kudya chitumbuwacho. Ine ndimangotaya njereyo, ndi kumangopitirira kumadya chitumbuwacho. Mukuona? Ndikapeza fupa la nkhuku; sinditaya nkhukuyo. Ndimangotaya fupalo.

25 Chotero, bwanji ngati nditanena chinachake chimene inu simungagwirizane nacho, nthawi iliyonse? Umangotaira gawo limenelo kutali. Ndipo, koma, uyang'ane pa izo mwabwino kwenikweni, kuwonetsetsa kuti ndi fupa, tsopano. Mukuona? Ndiyeno mulole ndinenenso, ngati iyo ili Njere, kumbukirani, Iyo imabala Moyo watsopano. Chotero muziyang'an molimba kwenikweni, ndipo Ambuye adalitse.

26 M'bale Carl Williams ananena chinachake usiku wina za kumasuka, kupempherera odwala, zomwe zingakhale zabwino kwambiri. Ndikudziwa kuti izo zingakhale zabwino. Koma ife basi. . . ife sitinakonzedwere pano kwa zimenezo, kuti tizibweretsa mzere wa pemphero. Ndipo ine sindikudziwa ngati M'bale Oral, kapena aliyense wa abale ena anakhalapo ndi mizere ya pemphero mmisonkhano yaikuluyi kapena ayi. Ine sindikudziwa. Ine ndayeserapo izo, kawiri kapena katatu. Koma, kawirikawiri, ngati gulu ngati ili, iwe umayenera kupereka makhadi a pemphero, mwaona, kuti uchite zimenezo. Chifukwa, inu simungathe. Lino si bwalo. Ndi nyumba ya Mulungu. Mukuona? Iyo inaperekedwa kwa izo. Ndipo ife . . . Iwo amakanikiza ndi kukankhana. Ndipo ukakhala ndi makadi, iwe umawafoletsa iwo pa mzere, mwadongosolo.

27 Chotero Billy anandifunsa ine, anati, "Kodi ndipite ndikapereke makadi? Anthu akundipempha ine makadi apemphero."

28 Ine ndinati, "Ayi, Billy. Tiyeni tingosiya Mzimu Woyera uchite zomwe Iye akufuna kuchita." Mukuona? Izo, mwaona, ndi kumulola Iye mwinamwake amange chikhulupiriro, ndi kungochiritsidwa apo pomwe pamene inu muli. Mukuona? Koma a . . . Mukuona?

29 Machiritso Auzimu ndi chaching'ono mu Uthenga. Ndipo inu simungathe kukhazikika pa chaching'ono. Aliyense akudziwa zimenezo. Koma iwo . . . Imeneyo ndi nyambo imene imagwiritsidwa ntchito kuti anthu akhulupirire mu Kukhalapo kwauzimu, kapena Mulungu, Chauzimu chiripo. Ndipo kenako, ndi zimenezo, ngati iwo angakhoze kuzindikira Kukhalapo Kwake, ndiye iwo amachiritsidwa, mwaona, mwa chikhulupiriro, kukhulupirira Izo.

30 Tsopano ndikufuna kuti ndiwerenge zina kuchokera m'Mawu a Mulungu, Chipangano Chatsopano. Ndiyeno ndikufuna kuti nditenge mutu wochokera ku Chipangano Chatsopano ichi, ndi Lemba ili, ndi kuyankhula madzulo ano pa phunziro kwa chabe—kanthawi pang'ono. Ndipo ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu motalika kwambiri ku misonkhano usikuuno. Koma kumbukirani, ndikuyembekeza kuti ndazipanga ndekha kumvetsedwa bwino. Mungozipatsa izo chidwi chanu kwa kanthawi, ngati inu mungathe.

Tsopano, ife tisanachite izi, tiyeni tiweramitse mitu yathu kachiwiri.

31 Inu mukudziwa, ife tikhoza kuyimba kwambiri. Ife tikhoza kufuula mochuluka kwambiri, mpaka ife kusasa mawu. Ndipo ife tikhoza kuyimba pa nthawi yolakwika, kapena kufuula pa nthawi yolakwika. Koma apa pali chinthu chimodzi, ife sitimachoka mu dongosolo pamene tikupemphera. "Ine ndikadakonda kuti amuna apemphere paliponse, atakwezera mmwamba manja oyera, mopanda kukayikira." Kapena . . .

32 Atate, ndi mwayi waukulu kwambiri umene munthu anakhalapo nawo, unali kutseka maso ake ndi kutsegula mtima wake, ndi kuyankhula kwa Inu. Ndipo ife tikudziwa kuti Inu mumamva, ngati titangokhulupirira kuti Inu mumamva. Pakuti Yesu anati, "Ngati inu muwapempha Atate chirichonse mu Dzina Langa, icho chidzaperekedwa." Izi zinali pa zoyenera kuchita, ngati sitidzakaikira izo. Chotero, Atate, tithandizeni ife kuti tikhulupirire, madzulo ano, kuti zopempha zathu ziperekedwe. Ndipo mulole pasakhale mthunzi umodzi wa kukayikira, paliponse. Koma mulole izo zichitike, zinthu zimene ife tikuzipempha. Ndipo izo ndi, Mulungu, kuti Dzina Lanu lalikulu lilemekezedwe lero, pobweretsa mu Ufumu Wanu moyo wotayika uliwonse ndi wosochera umene uli pansi pa kumveka kwa liwu lathu, kapena kumene tepi iyi idzakafikeko, uko mmaiko a achikunja, kumene kuzungulira dziko iwo akupita.

33 Ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti pasakhale munthu wofooka pakati pathu lero. Pamene msonkhano uzitha, mulole Ambuye Mulungu apulumutse mzimu wotayika uliwonse, ndi kuchiritsa thupi lirilonse lodwala, ndi kudzadza mtima wa ana Ake ndi chisangalalo. Ndi chifukwa chake tiri ndi chikhulupiriro, Ambuye, kuti tipemphe mu Dzina la Yesu,

kwa Mulungu Atate wathu, chifukwa Iye analonjeza kuti Iye adzamva. Ndipo izi ndi za kwa ulemelero Wake. Ameni.

34 Mu Uthenga wa Yohane Woyera, mutu wa 17, ndipo kuyambira ndime ya 20, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kwa—mutu. Ine ndikuganiza uko nkulondola.

> *Sindikupempherera awa okha, koma kwa iwonso amene adzakhulupirira pa ine ndi* mawu *awo;*
>
> *Kuti*. . .

35 Ndikukhulupirira kuti ndapeza malo olakwika. Tsopano, ndikhulululukireni mphindi chabe. Ine ndikufuna pemphero la Yesu limene. . .Kapena, osati pemphero la Yesu, kani, koma la Iye. . .Ine mwina ndalemba apa pa mutu wanga chinachake cholakwika. Ndi pamene Yesu anapemphera kuti. . .kapena ankanena kuti monga mkazi mu zowawa za kubala kwa mwana wake, kubala, kubala kwa mwana.

36 Izo ziri mu Luka kapena Yohane? Jack, izo ziri pati? [Wina akuti, "Yohane 16."—Mkonzi]. wa 16 wa Yohane. Ndimaganiza kuti zimenezo zinali zolondola, koma izo sizinamveke ngati choncho. Wa 16 wa Yohane. ["Ndime ya 21."] Ndime ya 21. Ndithudi, ndime ya 21. Ndithudi. Apa ife tiri. Yohane, Yohane Woyera 16:21.

> *Kuti iwo*. . .*mwina*. . .

37 Ayi, M'bale Jack, izo nzolakwikabe. [Winawake akuti, "Tayeserani Yohane, ndime 21." Wina akuti, "21." Wina akuti, "ndime ya 21 ya 16." Wina akuti, "16."—Mkonzi]. Ndi twente-. . . 16:21.Ine ndiri ndi mutu wa 16 wa Yohane Woyera, ndime ya 21. Koma iyo. . .Kodi ine ndikulakwitsa? [M'bale akuti, "Zowawa za mkazi, ndicho chimene iyo ili."]

[M'bale Branham akufotokoza za kumatana mu Baibulo ili pa tepi, *Lero Lemba Ili Lakwaniritsidwa* 65-0219—Mkonzi].

38 Chabwino, pali kusokonezeka mu ili. . .kumatana mu Baibulo ili. Inde, bwana. [M'bale akuti, "Iwo—iwo alisindikiza ilo molakwika."—Mkonzi]. Iwo analisindikiza ilo molakwika. Inde, bwana. Inu mukudziwa chiyani? Izo ndi ndendende zoona. Ili ndi Baibulo latsopano. Ine ndangolipeza kumene. Ndipo ilo liri—ilo liri. . .Ilo linasindikizidwa molakwika.

39 [Arkibishopu wa Katolika John S. Stanley akupereka Baibulo lake kwa M'bale Branham, ndipo akuti, "Mungo—mungokoka mpweya. Pali chifukwa chimene izo zachitikira, ndipo inu mukudziwa zimenezo, ndipo Mulungu akuwonetsani inu chinachake choti mutulutse mu izi, zimene ziri zopambana."—Mkonzi].

Chabwino.

["Ingogwiritsani ntchito langali apa, M'bale Branham."]

Zikomo inu. Zikomo inu, kwambiri. 16:21. Zikomo inu, kwambiri. Izo nzoona.

> *Mkazi pamene iye . . .*
>
> *Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Kuti* inu *mudza*gona, *kulira ndi kubuma, koma dziko lapansi lidzakondwera: ndipo mudzakhala achisoni, . . . chisoni chanu chidzasanduka chisangalalo.*
>
> *Mkazi pamene iye ali—ali mu zowawa* amakhala *ndi chisoni, chifukwa ora lake* likudza*: koma mwamsanga pamene iye abala mwana, iye sakumbukiranso . . . kuwawa—kuwawa, chifukwa cha chimwemwe kuti munthu wabadwa mu dziko lapansi.*

40 Zikomo inu, kwambiri, m'bale wanga. Ine ndithudi ndikuyamikira zimenezo.

41 Tsopano, uko ndithudi ndi kusindikiza kolakwika umu mu Baibulo; tsambalo layikidwa molakwika. Ndipo ine ndinangozipeza izo mu Baibulo langa lakale la Scofield, ndipo ndinanyamula ili ndi kuthamangira kuno ndi ilo, mphindi zochepa chabe zapitazo, chifukwa mkazi wanga wangondipatsa ine ili ngati mphatso ya Khrisimasi.

42 Tsopano, ine ndikufuna kuti—kuti ndiyankhule madzulo ano pa phunziro limene ine ndinalengeza: *Ululu Wa Kubala*. Tsopano, izo zikumveka moyipa kwambiri, koma izo ziri mu Baibulo.

43 Ine ndikukhulupirira kuti Yesu apa anali kuyankhula zimenezo, pamene Iye anati, "Inu mudzakhala ndi chisoni, koma chisoni chanu chidzasanduka chimwemwe," akuyankhula kwa ophunzira Ake apa, podziwa kuti kubadwa kwa—kwa Chikhristu kunkabwera mu kukhalapo. Ndipo tsopano zakale zikuyenera kufa, kuti zatsopano zibadwe. Kuti mukhale ndi chirichonse chimene chimabala, pamayenera kukhala ululu wa kusautsika. Ndipo iwo ndithudi anali oti adutse mu ululu wa kusautsika ndi zowawa, kuti achoke ku lamulo kupita ku chisomo.

44 Kubadwa kwabwino, kwachirengedwe kumayimira Kubadwa kwauzimu. Zinthu zonse zachirengedwe ndi zoyimira zauzimu. Ndipo ife tikupeza, ngati ife tingayang'ane kunja kuno—pansi, ndi kuwona mtengo mu nthaka, ukuphuka, ukuvutikira moyo. Izo zikusonyeza kuti pali mtengo, penapake, umene sumafa, chifukwa iwo—iwo ukulirira chinachake.

45 Ife timawapeza anthu, ziribe kanthu kuti ndi okalamba bwanji, odwala bwanji, chikhalidwe chotani, iwo amalira, kuti akhale moyo, chifukwa izo zimasonyezera kuti kuli moyo kwinakwake kumene ife timakhala moyo, tikakhala kwamuyaya. Zindikirani momwe ziriri zangwiro.

46 Tsopano, mu Yohane Woyamba 5:7, ine ndikukhulupirira ndi pamenepo, ngati ine sindikulakwitsa, Iyo inati, "Pali atatu amene amachitira umboni Kumwamba: Atate, Mawu, ndi Mzimu Woyera; atatu awa ndi Mmodzi. Pali zitatu zimene zimachitira umboni pa dziko lapansi, ndizo madzi, Magazi, ndi Mzimu, ndipo zimagwirizana mu chimodzi." Tsopano zindikirani. Zitatu zoyambazo *ndi* Mmodzi. Zitatu zachiwiri ndi zapadziko lapansi, zimene *zimagwirizana* mu chimodzi. Simungakhale ndi Atate popanda Mwana; simungakhale ndi Mwana popanda kukhala ndi Mzimu Woyera. Koma inu mukhoza kukhala ndi madzi popanda Magazi, ndi Magazi popanda Mzimu.

47 Ine ndikuganiza, kudutsa mmibadwo yathu, zatsimikizira izi kukhala zoona; madzi, Magazi, Mzimu; kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Izo zikuyimira, kapena zimapanga...kapena, ndi choyimira, chimene chimachotsa ku kubadwa kwachirengedwe.

48 Muwone pamene a—mkazi kapena chirichonse chikakhala mu ululu, wa kubala. Chinthu choyamba chimene chimachitika, ndi kutuluka kwa madzi, kubadwa kwabwinobwino; chinthu chachiwiri ndi magazi; ndipo kenako moyo umabwera. Madzi, magazi, mzimu; ndipo zimenezo zimapanga kubadwa kwabwinobwino, kwachirengedwe.

49 Ndi momwemonso izo ziri mu dera lauzimu. Ndi madzi; kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro, kukhulupirira pa Mulungu, kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu, ndi kubatizidwa. Chachiwiri, ndi kuyeretsedwa kwa mzimu, kuti Mulungu amayeretsa mzimu ku zinthu zonse za dziko lapansi, ndi chilakolako cha dziko lapansi. Ndipo kenako Mzimu Woyera umadzalowa ndi kudzapereka Kubadwa kwatsopano ndipo umazadzadza chotengera choyeretsedwa chimenecho.

50 Mwachitsanzo, monga chonchi. Tsopano, izo, ine ndinakuuzani inu. Chimene inu simukuchikhulupirira, chiyikeni pambali, mukatero mutenge chitumbuwacho. Zindikirani. Tsopano, a—tambula ikakhala kuti ili kunja kubwalo la nkhuku. Inu simumangoyitola iyo ndi kudzaiyika patebulo lanu ndi kuyidzazitsa ndi madzi kapena mkaka. Ayi. Mukaitola iyo, ndiko kulungamitsidwa. Kuiyeretsa iyo, ndiko kuyeretsedwa, chifukwa liwu la Chigriki *kuyeretsa* ndi liwu la pawiri, limene limatanthauza "kuyeretsedwa, ndi kuyikidwa pambali ku utumiki." Osati *mu* utumiki; *ku* utumiki. Ndiye mukaidzadza iyo, iyo imayikidwa mu utumiki.

51 Mukhululuke ichi tsopano, osati kuti ndikupwetekeni. Apo ndi pamene inu a Pilgrim Holiness, Anazarene mumalephera kuyenda mpaka pa Pentekoste. Inu munatsukidwa ndi kuyeretsedwa; koma pamene inu munakonzeka kuti mugwiritsidwe ntchito, mwa mphatso za kuyankhula mmalirime ndi zinthu zina, inu munazikana izo, munakagweranso mmbuyo

mu khola kachiwiri. Mukuona? Tsopano, ndizo—ndizo zimene zimachitika. Izo nthawizonse zimachita zimenezo.

52 Tsopano, osati kuti ndikutsutseni inu tsopano, koma basi ine—ine ndikufuna kuchichotsa ichi mu mtima mwanga. Ndipo icho chakhala chikundiwotcha ine nthawi yonse imene ine ndakhala ndiri kuno, kotero ine ndikhoza kungotero. Basi, ngati chisomo cha Carl, ndi Demos ndi iwo, ndi cha inu nonse, ine—ine ndiyesetsa mwakukhoza kwanga kuti ndipulumutse moyo wanga kwa izo, mwaona, ndiye izo ziri ndi inu.

Mwabwinobwino, kuyimira zauzimu.

53 Tsopano, ife tikupeza ndiye, ndipo iye wabadwa kwathunthu. Pamene mwana, kawirikawiri . . . Tsopano pamene madzi atuluka, inu simusowa kuchita zambiri za izo. Ndipo magazi akatuluka, inu simumasowa kuti muchite zambiri za izo. Koma, kuti mulowetse moyo mwa mwanayo, inu mumayenera kumumenya iye, ndi kumupangitsa iye kuti alire. Ndipo ndicho . . . Tsopano, opanda maphunziro, monga abale anga pano ndi ophunzitsidwa bwino kwambiri ku izo, zawo, koma ine ndimayenera kuti nditenge chirengedwe kuti ndifanizitse izo. Ndipo ndi inu pamenepo. Ndi chimene chinachitika. Izo zinatengera kumenya kwenikweni, kuti zifikitse ichi kwa iwo.

54 Tsopano, inu mutenge pang'ono, mtundu wina wa kugwedezeka. Mwinamwake, simusowa kuti mumumenye iye, koma kungomugwedeza iye pang'ono. Lingaliro kumene la iye kubadwa, nthawizina, lidzachita izo. Kumugwira iye, kumugwedeza iye. Iye akapanda kuyamba kupuma, mmenyeni iye pang'ono, ndipo kenako iye amayatsamula, mu malirime osadziwika, kwa iyemwini, ine ndikuganiza. Koma, iye—iye, mulimonse, ndipo iye amapanga phokoso.

55 Ndipo ine ndikuganiza ngati mwana abadwa mwa basi—wabadwa wakufa, wopanda phokoso, wopanda kugwedezeka, ameneyo ndi khanda lakufa.

56 Ndiro limene liri vuto ndi mpingo lero, kachitidwe; ife tiri ndi ana ambiri obadwa akufa. Uko nkulondola. Iwo akusowa kumenyedwa kwa Uthenga, inu mwaona, ndipo chotero kuti muwadzutse iwo, kuwabweretsa iwo kwa iwoeni, kuchitira kuti Mulungu athe kuwuzira mpweya wa Moyo mwa iwo. Ndipo tsopano ife tikupeza kuti izo nzoona kwambiri. Ndi fioloje yakhambi, koma ndi Choonadi, mulimonse.

57 Chotero, zindikirani, mu kubadwa kwa mbewu, mbewu yakaleyo ikuyenera kufa yatsopanoyo isanabadwe. Chotero, choncho, imfa ndi yovuta, nthawi iliyonse. Chotero, iyo imakhala yopweteka. Iyo imakhala yosimidwitsa. Kubadwa ndi chimodzimodzi, chifukwa iwe ukubweretsa moyo mdziko, ndipo ndiko—ndi kopweteka.

58 Yesu ananena kuti Mawu Ake anali Mbewu imene wofesa anapita kukaifesa. Tsopano, ife tonse tikuzidziwa zimenezo. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiphunzitse izi monga phunziro la Sande sukulu, chifukwa ndi Lamlungu. Zindikirani, ndiye, Mawu awa, pokhala Mbewu. Koma, kumbukirani, a—mbewuyo imangobweretsa moyo watsopano pamene iyo ikufa.

59 Ndi chifukwa chake izo zinali zowavuta kwambiri kuti Afarisi amenewo amumvetse Ambuye wathu Yesu Khristu, chifukwa iwo anali pansi pa lamulo. Ndipo lamulo linali Mawu a Mulungu mu mawonekedwe a mbewu. Koma pamene Mawu anadzasandulika thupi, ndipo nkudzakhala, osati lamulo, koma chisomo. Tsopano, chisomo ndi lamulo sizingakhalepo nthawi imodzi. Chifukwa, chisomo chimakhala pamwamba kwambiri pa lamulo, lamulo silimakhalapo nkomwe mu chithunzi. Ndipo chotero zinali zowavuta kwambiri Afarisi kuti afe ku lamulo lawo, kotero kuti chisomo chikhoze kubadwapo. Koma ilo likuyenera kupita. Malamulo awiri sangakhalepo nthawi imodzi.

60 Sipangakhale lamulo lonena kuti inu mukhoza kudutsa pa magetsi awa, ndipo lina nkuti inu mukhoza kudutsapo; lina lonena kuti inu mukhoza, lina nkuti simungathe. Iwo, ilo likuyenera kukhala lamulo limodzi pa nthawi. Mwinamwake nthawi ina inu munadutsapo; chenjezo, dutsanipo. Koma nthawi ino ilo lafiira. Imani! Mukuona? Ndipo chotero sipangakhale malamulo awiri pa nthawi imodzi.

61 Tsopano, ife tikuzindikira kuti izo nthawizonse . . . Lingaliro langa tsopano kwa inu, zimatengera kupweteka, kupsyinjika, kusautsika. Taonani momwe Afarisi amenewo anafera ku lamulo limenelo, kudzera mu zowawa, kupsyinjika, kusautsika. Koma izo zikuyenera kukhala.

62 Tsopano, ife tikupeza kuti mvula imene imabweretsa chipatso pa dziko lapansi, "Iyo imabadwa," monga wandakatulo anati, "mminda ya mabingu, mu mlengalenga mosawoneka bwino, molimba." Koma ngati tikanati tisakhale ndi mabingu ndi mlengalenga mosawoneka bwino, molimba, dontho laling'ono losungunuka la mvula limene lachotsedwa mnyanja ndi kudzasungunuka kuchokera mu mchere, ilo silingabadwe. Zimatengera mphezi, kuphulika kwa bingu; chinthu chosawoneka bwino, cholimba, chowopsya, kuti chibweretse madontho ofewa a madzi. Zimatengera ululu kuti ubale kubadwa. Zimatengera kufa. Ndipo pamene mitambo ikufa, mvula imabadwa, chifukwa mvula ndi gawo lya mtambowo. Wina ayenera kuchokapo kuti winayo akhalepo.

63 Tsopano, ndipo abale anga apa, ena a iwo anali okhoza, iwo akanakhoza kukupatsani inu malamulo onse a zinthu zimenezo. Ine sindingathe.

64 Tsopano tiyeni tigwere ku chinthu china, kungotsimikizira pang'ono chabe. Ine ndikuganiza limodzi mwa maluwa okongola kwambiri. . . Aliyense ali ndi malingaliro ake pa iwo. Koma ine ndikuganiza kuti duwa lokongola kwambiri limene ine ndinaliwonapo pafupi, ndi uko kummawa, kakombo wathu wa padziwe. Ndi angati anayamba amuwonapo kakombo wa padziwe? Oh, palibe china chonga iye, kwa ine. Koma kodi munazindikirapo chimene kakombo wa padziwe ameneyo amayenera kukhala? Ndikuganiza za chimene Yesu ananena, "Lingalirani kakombo, momwe amavutikira ndi kudzipota, komabe Ine ndinena ndi inu, kuti, Solomoni mu ulemelero wake wonse sanavekedwe monga mmodzi wa awa." Pakuti, ulemelero wa Solomoni ndi zovala zake zonse zinali zongopanga. Koma kakombo, mu kukongola kwake, muli moyo umene umamupangitsa iye kukhala wokongola, osati zozipanga zopaka, kuyika penti.

65 Chimodzimodzi monga akazi athu, sindikuganiza kuti inu mumayenera kukhala ndi zobiriwira zonsezi, inu mukudziwa, ndi nsize za mmaso, inu mukudziwa, kunja monga choncho, ndi zodzikongoletsera zonsezo kapena—kapena osati, ine ndimasokoneza zinthu zimenezo, zonse pa nkhope yanu, kuti zikukongoletseni inu. Kukongola ndi momwe kukongola kumachitira. Ngati mungawonjezere Machitidwe 2:4 pang'ono, kumusakaniza zonse pamodzi, ndi Yohane 3:16 pang'ono, izo zidzaposa chirichonse chimene Max Factor anayeserapo kuchipanga. Mukuona? Mwamuna wanu adzakukondani inu kwambiri; wina aliyense adzatero; ndipo ndikutsimikiza kuti Mulungu adzatero.

66 "Kakombo," Iye anati, "lingalirani iye, momwe iye amakulira, kuvutika, amayenera kudzibweretsa yekha pamwamba." Kakombo wamng'ono wa padziwe uyu, onani kumene iye anachokera; mdothi, ndowe, matope, madzi amatope, madzi akuda. Iye anakankhira njira yake kudutsa mu zonsezo, nyongolosi yaying'ono iyi ya moyo, kudzigwirira yekha ntchito kuchokera pansi pa dziwe kumene achule ndi—ndi zinthu zimakhalako, ndipo kenako nkudzibweretsa yekha kudutsa mu zonsezo. Koma pamene iye afika mu kukhalapo kwa dzuwa, iye amabadwa. Mbewu yaing'onoyo imaphulika nkutsegukira ku moyo. Iyo singachite izo mpaka itadutsa mu njira yonseyo. Iyo ikuyenera kubwera kudutsa zimenezo. Izo ndi zimene zimamupanga iye, ndi chifukwa chakuti dzuwa lenilenilo ndi limene likumukoka iye. Ndipo pamene iye afika mokwanira pamwamba pa madzi onse akuda, ndi matope, ndi zina zotero, ndiye iye amasangalala kwambiri, iye amangopereka moyo wake momasuka. Ndipo ndi moyo wokongola pamene iye afika mu kukhalapo kwa chimene chikumukoka iye.

67 Ine ndikuganiza kuti uwu ndi mtundu wokongola wa moyo wa Chikhristu. Pamene, Chinachake chikukukokani inu

kuchoka mdziko, mpaka tsiku lina inu mudzabadwa mu kukhalapo Kwake komwe, mwa Mzimu Woyera. Ndi zokongola bwanji! Ngati muyesera kuti muchithandizire icho, muchipha icho.

68 Monga mwanapiye pamene iye akubadwa, inu mukudziwa, ngati inu munayamba mwazindikirapo mmodzi wa tating'onoto, pamwamba pomwe pa mlomo wake waung'ono, kapena mbalame iliyonse imene imabadwa kuchokera ku dzira. Icho—icho chikuyenera. . .Icho chikukhwima, chikhungwa cha dzira chakale ichi. Gawo lakale lamkati mwa mazira likuyenera ku—kuvunda. Ndipo iye akuyenera kutenga mlomo wawung'ono uwu, ndi kumakanda mmbuyo ndi mtsogolo mpaka iye ataswa chikhungwacho. Ife timazitcha izo, kusuzumira njira yake yotulukira, kumusi ku Kentucky kumene ine ndimachokerako. Kusuzumira njira yake yotulukira. Iwo sanapezepo njira yabwinoko. Mukuona? Mukuona? Bwanji? Ndi njira yoperekedwa ndi Mulungu. Mukayesera kuti mumuthandizire iye, inu mudzamupha iye. Kugogomola chikhungwacho pa iye, iye afa. Mukuona? Iye amayenera kuti avutikire, kupsyinjika, akamatuluka.

69 Umo ndi momwe Mkhristu akuyenera kuchitira. Si winawake akungogwira dzanja lanu, kukutengerani inu mkati. Inu mukuyenera kukhala pamenepo mpaka inu mutafa, kuvunda, ndi kubadwira mu Ufumu wa Mulungu. Ndiyo njira yoperekedwa ndi Mulungu. Inu simumalowa ndi bukhu, kapena kugwirana chanza, ndi kujowina, kupopera mmwamba, kukokera pansi. Inu—inu mumangoyenera kuchoka ku chikhungwa chakalecho. Zindikirani, palibe njira ina yabwinoko imene iwo anayamba ayipezapo.

70 Iwo sanapeze njira ina yabwinoko yoti mwana azipeza zimene akufuna pambali pa njira ya Mulungu yochitira izo. Tsopano, pamene mwana wamng'ono ameneyo abadwa, inu mukhoza kuyika belu pansi apa pambali pa kabedi kake kakang'ono, nkumuuza, "Mwana wanga wamng'ono, ndine a—wa fioloje mnjirayi. Ine ndawerengapo mabukhu a momwe ndingalerere mwana. Ndipo, ine ndikukuuza iwe, ndiwe mwana wamakono. Iwe unabadwira m'nyumba yamakono, ndi kholo lamakono. Ukakhala ndi njala, kapena ukufuna amayi kapena ine, uzingoyimba kabelu kakang'onoka." Izo sizingagwire ntchito nkomwe. Njira yokhayo yomwe iye angapezere chimene akufuna, ndi kulirira icho. Imeneyo ndi njira ya Mulungu.

71 Ndipo ndiyo njira imene timapezera zomwe tikuzifuna, ndi kulirira izo. Kulira momveka. Osachita manyazi. Kumati, "Ndikumuchitira njala Mulungu." Ziribe kanthu kaya ndi madikoni, azibusa, kapena aliyense amene ali pafupi, fuulani, mulimonse. A Jones akhala pamenepo; zipanga kusiyana kotani? Lirani mofuula, ndiyo njira yokhayo yopezera izo, mpaka mutapeza thandizo. Iye anaphunzitsa zimenezo pamene Iye

anali kuno pa dziko lapansi, inu mukudziwa, za woweruza wosalungama.

72 Dontho la mame laling'ono, sindikudziwa kapangidwe kake. Mwinamwake pangakhale sayansi pano ya . . . Ine ndingonena momwe ine ndikuganizira. Ilo likhoza kukhala mtundu wina wa gulu lopanikizikana la mlengalenga litabwera pamodzi mu usiku wamdima, ndipo ilo limagwera pa dziko lapansi. Ndipo pamene ilo litero, ilo limabadwa mu usiku. Koma m'mawa, ilo limakhala pamenepo, litazizidwa, ndi kumanjenjemera, pa tsamba laling'ono la udzu, kapena kupachikika pa chingwe cha zovala zanu. Koma mungolola kuti dzuwa liwale kamodzi, kodi munazindikirapo momwe limakhalira losangalala? Ilo limangonyezimira ndi kunjenjemera. Chifukwa chiyani? Ilo limadziwa kuti kuwala kwadzuwa kulikokeranso ilo kumene linali pachiyambi.

73 Ndipo chomwechonso amatero mwamuna kapena mkazi aliyense amene wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Pamakhala chinachake cha izo, pamene Kuwala kufalikira pa ife, kuti ife timakhala okondwa, chifukwa ife timadziwa kuti ife tikubwerera kumene ife tinachokerako, kuchokera ku chifuwa cha Mulungu.

74 Ilo likhoza kunyezimira ndi chisangalalo, pamene dzuwa lamenya ilo, ndithudi, podziwa kuti likupita kumene linachokerako.

75 Zinthu zazing'ono zakhambi, koma ife tikhoza kumapirira nazo, koma tiyeni tipeze chinthu china.

76 Ife tikudziwa mbewu yakale ili, ikuyenera, mbewu yatsopanoyo isanatuluke kuchokera mu mbewu yakaleyo, iyo imayenera kuti ivunde, mwamtheradi. Osati kufa, kokha, koma kuvunda iyo itafa. Ife tikudziwa kuti izo nzoona.

77 Ndicho chinthu chomwecho mu Kubadwa kwatsopano. Sitimabwerera mmbuyo, koma timapita patsogolo pamene wabadwa mwatsopano. Ndipo ndi chifukwa chake ndikuganiza, lero, ife tiri ndi (kochuluka) osati kochuluka, kani, Kubadwa kwatsopano kwenikweni, ndi chifukwa chakuti mbewu ili, mwinamwake, idzamvera chisoni Mawu kapena munthuyo, koma iwo sakufuna kuvunda kuchoka ku kachitidwe kakale kamene iwo analimo. Iwo safuna kuti atulukemo mmenemo. Iwo amafuna kuti azikhala mu kachitidwe kachikale, ndi kudzinenera Kubadwa kwatsopano, kapena Uthenga wa m'badwo. Ife tinazipeza zimenezo pansi pa Luther, Wesley, Apentekoste, ndi mibadwo ina yonse. Iwo akuyesetsabe kugwiritsitsa ku kachitidwe kachikale, ndi kumadzinenera Izi. Koma m'badwo wa kachitidwe kachikale ukuyenera kufa, kuvunda, kuti pabwere watsopano. Iwo akufunabe kumamatira.

78 Zindikirani. Iwo amadziwa kuti kachitidwe kachikale kanafa, koma iwo samafuna basi kuti avunde mu zimenezo.

Tsopano, kuvunda, ndi pamene icho chathetsedwa kwenikweni. Pamene a . . . *Kudzinenera* kupangidwa, kuti iwo ndi Obadwa mwatsopano, koma kudzinenera ndi chizindikiro chobadwa. *Kuvunda,* kumabweretsa Kubadwa kwatsopano. Tikuyenera kuvunda ku izo, monga ife tinachitira mu mibadwo yonse, kudutsa wa Achiwesile, ndi ena onse.

79 Koma, chinthu chake ndi chakuti, zitatha izo, Kubadwa kwatsopano kumabadwa. Wesley kapena . . . Luther anabwerapo ndi mawu amodzi, "Olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro." Chabwino, iye sakanatha kumamatiranso ku kachitidwe kachikale. Iye ankayenera kuti atulukemo.

80 Ndipo kenako pamene Achikalvini anawufikitsa mpingo wa Anglican mu chikhalidwe choterocho, pansi pa chiphunzitso cha Chikalvini, mpaka Mulungu anadzutsa chiphunzitso cha Arminiya, chimene anali John Wesley. Kachitidwe kachikale kankayenera kufa, kuti katsopano kabwerepo.

81 Ndipo pamene m'badwo wa Wesley unatha, ndi mibadwo yaing'ono yonse, kapena masamba amene anatulukira pa phesi, kapena ngayaye, mu nthawi ya Wesley . . . Mwaona, pamene Pentekoste inatulukira ndi kubwezeretsa kwa mphatso, iwo ankayenera kuti atuluke mu Baptisti, Presbateria, Pilgrim Holiness, Nazarene, Mpingo wa Khristu (wotchedwa), ndi zonsezo. Iwo ankayenera kuti atuluke mu izo, kuvunda kuchoka kwa izo, kuti avomereze Kubadwa kwatsopano.

82 Inu nthawizonse mumatchedwa openga. Koma izo ziri monga momwe Paulo ananenera pamene anavunda pa chimene iye ankadzinenera poyamba. Anati, "Munjira imene imatchedwa mpatuko, umo ndi momwe ndimamupembedzera Mulungu wa makolo athu." Munjira imene imatchedwa mpatuko! Mukuona? Iye anali atavomereza Moyo watsopano, kuti Chipangano Chakale chinali chitabala Chatsopano, ndipo iye ankayenera kuvunda kuchoka ku Chakale ndi kungochipanga icho mthunzi. Kuti akhale . . .

83 Apo ndi pamene ife tiri tsopano. Tsopano, mupirire nane. Koma limenelo ndi lingaliro langa. Mipingo yachita mwadongosolo kwambiri mpaka iwe sungathe kulowa mu wina pokhapokha iwe uli wa winawo. Iwe uyenera kukhala ndi khadi la chiyanjano, kapena mtundu wina wa chokuzindikiritsa. Ndipo pokhulupirira izi, khomo lokhalo limene ine ndiri nalo pafupifupi lotsegula ndi Amuna Amalonda awa. Ndipo bola ngati iwo sali bungwe, ine ndikhoza kumapita ndi iwo, koma, ndipo nkuyamba kubweretsa Uthenga, umene ine ndikumverera kuti uli pa mtima wanga, kwa anthu. Koma zachitika mwadongosolo kwambiri. Ndipo ine ndimakukondani inu anthu Achipentekoste. Ndipo pentekoste si bungwe, mulimonse. Inu mumangodzitcha nokha chomwecho. Pentekoste ndi chokuchitikira osati chipembedzo.

84 Koma, inu mukuona, chinthu chake ndi chakuti, zikumakhala zowavuta kwambiri amuna ambiri. Pamene iwo ayang'ana pa Iwo ndi kuwukhulupirira Iwo, ndi kuwuwona Iwo ukuzindikiritsidwa chomwecho ndi Mulungu, mu Mawu, komabe, zikumakhala zovuta kwambiri kuti muvunde kuchoka kwa chinthu chimene mwakhalamo. "Kodi ine ndikachita chiyani? Kodi ine ndikapeza kuti chakudya changa?"

85 Chiyani? Mulungu ndiye chakudya chanu. Mulungu ndiye chinthu choti inu mugwireko. "Funani poyamba Ufumu wa Mulungu, ndi chirungamo Chake." Ndizisiya izo zikhale pamenepo. Inu mukudziwa chimene ine ndikunena.

86 Ife timauzidwa ndi aneneri a Mulungu kuti tikuyenera kukhala ndi dziko lapansi latsopano, Kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano. Ngati inu mukufuna Lemba la zimenezo, ndi Chivumbulutso 21. Ine ndikhoza kuwerenga ilo mobwereza kwa inu, ndiri nalo ilo apa. Yohane anati, "Ndinawona Kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano: pakuti kumwamba koyamba ndi dziko loyamba zinachoka." Izo zinali zitapita. Tsopano, ngati titi tidzakhale ndi dziko lapansi latsopano, dziko lapansi lakale ndi dziko lapansi latsopano sizingakhalepo nthawi imodzi. Kapena, dziko latsopano ndi dziko lakale sizingakhalepo nthawi imodzi. Sipangakhale maulamuliro awiri a dziko pamodzi nthawi imodzi. Tsopano, kuti titenge dziko lapansi latsopano, lakale likuyenera kufa. Tsopano, ngati lakale likuyenera kuti life, ndiye ilo likupereka ululu wa kubala kwa latsopanolo tsopano.

87 Ndiyeno ngati dokotala atapita kuti akamupime wodwala amene anali mu zowawa tsopano, a. . .chimodzi cha zinthu zimene dokotala ameneyo angachite. Chimene, ine ndikuyankhula pamaso pa awiri kapena atatu, ine ndikudziwa, madokotala azamankhwala abwino pano, madokotala Achikhristu. Ndipo ine—ine—ine ndingakufunseni inu ichi. Chimodzi cha zinthu zoyamba chimene dokotala amachita, akatha kumuyang'anira wodwalayo, ndi kuwerengera ululu, ululu wa kubala. Iye amawerengera ululuwo, momwe iwo wayandikirana pamodzi, ndi kuchuluka kwa kuwopsya kumene uliwonse umafikapo. Wina ndi wovuta kukhala nawo kuposa winawo. Wotsatira, wovutabe, umafika moyandikana pamodzi. Umo ndi momwe iye amafufuzira vutolo, pogwiritsa ntchito ululu wa kubala.

88 Chabwino, ngati dziko likuyenera kupereka njira ku kubadwa kwa dziko latsopano, tiyeni tingofufuza ululu wa kubala wina umene tiri nawo padziko lapansi, ndipo kenako tiwona kuti ndi tsiku liti ndi momwe ilo latalikira mu kuvutika kwake.

89 Nkhondo Yoyamba Yapadziko inawonetsera ululu waukulu wa kubala. Iyo inawonetsera umodzi wa ululu woyamba wa

kubala kwake. Chifukwa cha nthawi imeneyo kwa iyo, ife tinali titabweretsapo mabomba, ndipo tinali ndi mfuti zamakina, ndi mpweya wachiphe. Ndipo inu mukukumbukira. Mwinamwake ambiri a inu simungathe. Ine ndinali mnyamata chabe wamng'ono wa pafupifupi zaka eyiti, koma ine ndikukumbukira iwo akuyankhula za mpweya wa mpiru uwu ndi klorini, ndi zina zotero. "Momwe zikungowoneka ngati ziyamba ndi," iwo anati, "izo zidzatentha dziko lonse lapansi. Zidzamupha aliyense. Chabwino, izo zikhoza kukhala a—a—kusweka kwa zimenezo, mphepo chabe zikungowomba izo kudutsa pa dziko lapansi." Ndipo momwe aliyense ankachitira mantha pafupifupi ngati afa ndi chida chachikulu chimenecho cha mpweya wachiphe! Dziko lapansi linadutsamo, linali ndi ululu wake wa kubala woyamba.

90 Ndipo ife tikupeza tsopano, ife tinali ndi nkhondo yachiwiri, nkhondo Yadziko Lonse, ndipo ululu wake unali wawukulu kwambiri. Izo zimakhala zowopsya kwambiri nthawi zonse, ululu wa kubala wa dziko lapansi. Ilo linali pafupifupi kuti ligonje, mu nthawi ya bomba la atomiki, chifukwa ilo likanawononga mzinda wonsewo. Zinali zazikulu kwambiri kuposa ululu wa Nkhondo Yoyamba Yapadziko lonse, za kuwonongedwa kwa dziko lapansi.

91 Tsopano, ilo likudziwa kuti nthawi yake ya chiwombolo yayandikira. Ndi chifukwa chake ilo liri lamanjenje kwambiri, lokhumudwa, monga ilo liri, ndi chifukwa chakuti pali bomba la haidrojeni, ndi mizinga ya mlengalenga imene ingawononge dziko lonse. Fuko lina likuchita mantha ndi limzake, ziribe kanthu momwe ilo liri laling'ono. Iwo ali ndi mizinga imeneyo imene iwo amati idzango. . .Imodzi ya iyo. Iwo akhoza kuilondolera iyo pogwiritsa ntchito nyenyezi ndi kuiponya iyo paliponse mdziko limene iwo akulifuna.

92 Russia, monga ine ndinamvera pa nkhani, tsiku lina, akudzinenera kuti akhoza kuliwononga dziko lino, ndi—ndi kusunga ma atomu kapena zinthu kuti zisawononge fuko lake. Ife sitikudziwa choti tichite ndi zimenezo. Aliyense akupanga zodzinenera zimenezi, ndipo ziri chomwecho.

93 Sayansi ya anthu yalowa mu labotare yaikulu ya Mulungu, mpaka iwo adziwononga okha. Mulungu amalola, nthawizonse amalola nzeru idziwononge yokha. Mulungu samawononga chirichonse. Munthu amadziwononga yekha ndi nzeru, monga iye anachitira pachiyambi, kutenga nzeru za Satana mmalo mwa Mawu a Mulungu.

Tsopano, ilo likudziwa kuti likuyenera lipereke njira. Ilo silingakhoze kupirira zimenezo.

94 Russia, ine ndikukhulupirira, angawononge fuko lino lero, ngati iye akuganiza kuti iye akhoza kuliwononga ilo, ndipo kenako nkudzipulumutsa yekha. Lirilonse la mafuko aang'ono

amenewo akhoza kuchita zimenezo. Koma, iwo akuchita mantha, chifukwa iwo akudziwa kuti dzikoli silingathe kuyima mu njira yake pansi pa zochitika zoterezi.

95 Chotero, dziko likudziwa kuti ululu wa kubala wake ndi waukulu kwambiri, ilo likuyenera kupereka njira. Pakhala pali kubadwa kwatsopano, kubadwa, kuli pafupi. Ndine wothokoza chifukwa cha izo. Ndatopa nalo ili. Aliyense... aliyense amadziwa kuti—kuti pano ndi malo a imfa ndi chisoni, ndi mitundu yonse ya chisokonezo, ndi zina zotero. Ndine wokondwa kuti ilo likuyenera kupereka njira, ndipo ndine wokondwa kuti nthawi yayandikira. Monga Yohane ananenera, wakale, "Ngakhale chomwecho, bwerani, Ambuye Yesu."

96 Tsopano, ilo likuyenera kuvunda, ndithudi, monga ine ndanenera, kuti libweretse kubadwa kwatsopano. Taonani chimene ilo lavundiramo. Zindikirani, abale anga! Ilo lavunda kwathunthu. Ndale zake ndi machitidwe ndi zovunda basi momwe zingakhalire. Palibe fupa labwino mwa ilo, mu machitidwe ake a dziko, ndale zake ndi ndale zake zachipembedzo, ndi chirichonse chimene icho chiri. Wina amati, "Ndine wa Democrat. Ndine wa Republican. Ndine wa Methodisti. Ndine wa Baptisti." Bwanji, chinthu chonsecho chavunda mpaka mkati. Pakuyenera kukhala chinachake choti chipereke njira. Ilo silingathe kuyima. Ngati inu mutamuyika George Washington kapena Abraham Lincoln mu boma lirilonse mu United States, ilo silingabwererebe. Ilo lapitirira chiwombolo.

97 Pali chinthu chimodzi chokha chimene chingalithandize ilo, ndicho Kudza kwa Mlengi. Ameni.

98 Ilo limadziwa kuti likuyenera kupereka njira. Ilo liri mu ululu ndi kupsyinjika. Lina silikudziwa choti lichite. Lina likuyang'ana mbali *iyi*, ndipo lina mbali *iyo*, ndi chirichonse. Lina likumuwopa mzake. Lina likuyesetsa kuti lichite chinachake chimene chidzawononge *ili*. *Ili* likuyesetsa kuti lidzitsutsana ndi *ilo*, kuliwononga linalo. Mpaka, tsopano iwo ali ndi izo mmanja mwa anthu ochimwa, amene akhoza kuliwononga dziko lonse mu maminiti asanu. Mukuona? Chotero ilo likudziwa kuti silingapirire izo. Anthu akudziwa kuti ilo silingapirire izo. Ndipo dziko likudziwa kuti iwo atero, izo zichitika.

99 Pakuti, Mulungu anati izo zinali. "Miyamba yonse ndi dziko lapansi zidzayaka moto." Padzakhala kukonzanso kwa chinthu chonsecho, kotero kuti dziko latsopano likhoze kubadwa. Mulungu analoseratu zimenezo.

100 Ilo lavunda, mu kachitidwe kake konse, ndipo ilo likuyenera kuti lichite zimenezo, kuti livunde.

101 Ndi chifukwa chake ilo, ine ndinati, ilo ndi lamanjenje kwambiri ndi lofiira pa nkhope, ndi lokhumudwa. Ndi zivomezi,

konsekonse, ndi chokwera-ndi-chotsika pa gombe. Ndi mafunde amphamvu mu Alaska, ndipo akugwedeza mokwera-ndi-motsika pa gombe, zivomezi ndi zinthu. Ndipo anthu akulemba, "Kodi ife tichokeko? Kodi ife tichokeko?" Mukuona? Iwo sakudziwa choti achite. Kulibeko malo otetezedwa koma Amodzi, amenewo ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo. Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chimene chiri malo otetezeka, ndipo ndicho Iye. Onse kunja kwa Amenewo adzawonongeka, motsimikiza basi monga Mulungu ananena chomwecho.

102 Tsopano tiyeni tiyang'ane pa Bukhu la Dokotala, ngati ilo liri mu mtundu uwu wa chikhalidwe, ndipo tiwone ngati izi zikuyenera kuchitika pamene dziko lapansi latsopano liti lidzabadwe. Mateyu 24, mu Bukhu la Dokotala, lomwe liri Baibulo, ndipo tiyeni tiwone zomwe zinaloseredwa, zomwe zidzakhale zizindikiro zake.

103 Tsopano, ngati dokotala adziwa zizindikiro za kubadwa kwa mwana. . .Ndipo nthawi yoti mwanayo abwere, iye amakonzekeretsa chirichonse, chifukwa iye amadziwa kuti imeneyo ndi—nthawi yoti mwanayo abadwe. Chifukwa, zizindikiro zonse zimasonyeza; a—madzi akutuluka, magazi. Ndipo tsopano. . .Nthawi yafika. Mwanayo abweretsedwe, ndipo ndi nthawi yoti mwanayo abadwe. Ndipo kotero iye amakonzekera chirichonse.

104 Tsopano, Yesu anatiuza ife ndendende basi zomwe zikanati zidzachitike pa nthawi ino. Iye anatiuza ife, mu Mateyu 24, kuti Mpingo, Mpingo woona, ndipo mpingo winawo, ukanadzakhala. . .Mpingo wachirengedwe, Mpingo wauzimu, "Ukanadzakhala woyandikana kwambiri limodzi, otsanzira, mpaka iwo ukanadzanyenga Osankhidwa omwe, ngati kukanakhala kotheka." Momwe izo zinakhalira mmasiku a Nowa, "Momwe iwo ankadyera, kumwa, kukwatira, kukwatiwa," ndi makhalidwe oyipa onsewa a mdziko amene tikuwawona lero. Baibulo, Bukhu, Bukhu la Dokotala linati izo zikanadzachitika. Chotero, pamene tiziwona izi zikuchitika, timadziwa kuti kubadwa kwayandikira. Izo zikuyenera kukhala. Inde, bwana. Tsopano, ife tikuyang'ana pa zimenezo, monga—monga fuko; osati monga fuko, koma dziko.

105 Tsopano, Israeli, mpingo, tiyeni tiyambire kumbuyo ndi iye maminiti pang'ono. Ndipo tiyeni timutsatire iye kwa maminiti teni otsatirawa, mwinamwake. Israeli amakhala ndi ululu wa kubala pansi pa mneneri aliyense amene ankabwera pa dziko lapansi. Iye amakhala ndi ululu wa kubala pa Uthenga wake. Pakuti kodi iye ankachita chiyani? Mneneriyo amakhala ndi Mawu. Ndipo—ndipo iye anali atafesa chivundi chochuluka ndipo anapanga madongosolo ochuluka mu umunthu wake, mpaka mneneri uyu ankamugwedeza iye kuchoka pa maziko ake. Iwo ankadedwa ndi aliyense. Chotero,

choncho, pamene Mulungu atumiza mneneri, mpingo pawokha unkapita mu ululu wa kubala. Chifukwa, mneneri, "Mawu a Ambuye amadza kwa mneneri, ndipo iye yekha." Ndiko kuti, Mawu amene anayankhulidwa kwa tsiku limenelo amawonetseredwa ndi mneneri wa m'badwo umenewo, nthawizonse zimakhala zikuchitika. Ndipo, mipingo, iwo amamanga machitidwe ochuluka kwambiri kuzungulira Mawu, mpaka iye ankawugwedeza iwo nkuwuchotsa pogwedezera pakepo pamene iye abwera. Iwo unkakhala ndi ululu wa kubala.

106 Chinali chiyani chimenecho? Kubwerera ku Mawu! Kubwerera ku Moyo! Kachitidwe sikamakhala ndi Moyo. Ndi Mawu a Mulungu okha amene amakhala ndi Moyo. Kachitidwe kamene kamamangidwa mozungulira Iwo, kumene kulibe Moyo. Ndi Mawu amene amapereka Moyo. Uthenga Wake unkamugwedezera wotsalira kubwerera ku Mawu. Gulu laling'ono limabwera ndi kudzakhulupirira. Nthawiyina, mwinamwake. . . Mu nthawi ya Nowa, pafupifupi anthu eyiti okha. Koma, mulimonse, Mulungu ankagwedeza wotsalirayo. Ndipo, nkuwawononga, ena onsewo amene ankayenera kusasidwira kutali.

107 Iwo ankachita izo, monse kudutsa mmibadwo, mpaka potsiriza mpingo unapereka kwa iwo Mwana Wamwamuna, ndipo Mwana Wamwamuna ameneyo anali Mawu, Iwoeni, atasandulika thupi. "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu." Iye anagonjetsa mdierekezi aliyense, mphamvu iliyonse pa dziko lapansi, imene inabwera momutsutsa Iye, ndi Mawu a Atate okha. Yesero lirilonse limene Satana anamupatsa Iye, Iye anamudzudzula Satana; osati ndi Zake—mphamvu Zake Zomwe zimene Iye anali nazo, koma ndi Mawu a Mulungu. "Kwalembedwa. . . Kwalembedwa. . . Kwalembedwa. . . " Pakuti Iye anali Mawu.

108 Pamene Satana anawuluka motsutsana ndi Eva, iye sanali Mawu, kotero izo zinalephera. Pamene iye anawuluka motsutsana ndi Mose, izo zinachita chinthu chomwecho. Koma pamene iye anagunda Mwana wa Mulungu, Iye anali mavolti teni sauzande. Izo zinathothola nthenga zomasuka pa iye, pamene Iye anadzabwerera ndipo anati, "Kwalembedwa, 'Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse otuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.'" Pamenepo panali Mwana Wamwamuna uja, atasandulika thupi. Mawu Amuyaya a Mulungu, Iyemwini, akuwonetseredwa mthupi la mnofu pano pa dziko lapansi, kuti akawaimirire Mawu.

109 Umo ndi momwe Iye ankadziwira zomwe zinali mmitima mwawo. Umo ndi momwe Iye ankakhoza kumuuza Filipo kumene iye anali, yemwe iye anali. Iye ankatha kumuuza

Simoni Petro yemwe iye anali. Anamuuza mzimayi pa chitsime. Chifukwa chiyani? Iye anali Mawu. Kulondola. Baibulo linanena, mu Ahebri mutu wa 4, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa, amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konse-konse, kudula molekanitsa mpaka mmafuta a fupa, ndi Wozindikira malingaliro ndi zokhumba za mtima.”

110 Bwanji, ansembe Achifarisi akhungu amenewo sankatha kuwona kuti Awo anali Mawu akuwonetseredwa, pakuti iwo anali atakulungidwa mu unsembe ndi kachitidwe. Ndipo kachitidwe kachikale kankayenera kuti kapereke njira. Iwo anali Mawu, koma zomwe zinali zitalonjezedwa zinali zitakwaniritsidwa. Kotero ngati izo zakwaniritsidwa, zikuyenera kuvunda. Ndi chikhungwa. Mbewu inkapitirira.

111 Mose sakanabweretsa uthenga wa Nowa. Ngakhalenso Yesu sakanabweretsa uthenga wa Nowa, chifukwa iwo unali m’badwo wina. Ndipo mbewu yakaleyo inali yolondola, koma iyo inatumikira cholinga chake ndipo inafa ndipo inapita. Kusintha kuchokera ku chakale kupita ku chatsopano, kumene Moyo unali, chinali chimene chinkawadetsa nkhawa anthu, chimene chikuwadetsa nkhawa iwo lero.

112 Ife sitikumanga khoma, monga ife tikuyambira ndi uthenga wa Luther, kumapita kumusi mu mzere wowongoka, kapena uthenga wa Chipentekoste. Kulondola. Ife tikukhota makona. Ife tikumanga nyumba. Mawu a Mulungu ndi pulani. Aliyense akhoza kumanga mzere wowongoka, koma pamafunikira mmisiri kuti apinde konayo. Zimatengera mphamvu ya Mulungu kuti ichite zimenezo. Zimatengera wodzozedwayo kuchokera Kumwamba, kuti adzatumizidwe pansi kuti adzachite zimenezo. Izo zimatero, mu m’badwo uliwonse. Ndipo mu m’badwo wa mneneri, Mawu a Ambuye amabwera kudzera mwa aneneri amenewo, ndipo iwo amakhota makona amenewo, ankapanga kusiyana kumeneko. Koma omangawo ankafuna kumanga khoma. Si khoma, konse, ndi nyumba, nyumba ya Mulungu.

113 Tsopano, ife tikumverera ndipo tikudziwa kuti Ichi ndi Choonadi, kuti machitidwewo amavunda mu m’badwo uliwonse. Ndipo kalikonse ka kachitidwe kawo kankayenera kuvunda ndi kufa, mpaka iye anawubweretsa Mpingo umenewo. Kuchoka mu nyansi zovundazo panabwera Mawu, Iwoeni. “Mawu a Ambuye amadza kwa aneneri.” Samabwera konse kwa ansembe; Iwo amabwera kwa aneneri.

114 Ndipo zindikirani, ndipo pamene Iwo anatero, potsiriza Mawu amenewo palimodzi anadzabadwa umu mu thupi la munthu. Chidzalo cha Umulungu mu thupi chinadzakhazikika mwa Iye. Iye anali Mawu. Aneneri amakhala gawo la Mawu, Mawu a m’badwo wawo. Ife, lero, ndife gawo la Mawu, amene timatsatira Mawu. Koma Iye anali chidzalo chonse cha Mawu. Iye anali Mawu. Iye anati . . .

115 Pamene iwo ankamuyimba mlandu Iye, akudzipanga Iyemwini wofanana ndi Mulungu, chifukwa Iye anali Mwana wa Mulungu, iwo anati kwa Iye, "Chabwino, Iwe ukudzipanga Wekha Mulungu."

116 Iye anati, "Kodi izo sizinalembedwe mmalamulo anu, kuti mumawatcha iwo amene Mawu a Mulungu anabwera kwa iwo, 'amulungu,' aneneri? Ndipo iwo anali. Ndiye inu munganditsutse bwanji Ine pamene Ine ndikuti Ine ndi Mwana wa Mulungu?"

117 Kumene, chidzalo cha Umulungu mthupi chinakhala mwa Mwana wa Mulungu. Iye anali mawonetseredwe athunthu a Mulungu. Chimenecho ndi chimene potsiriza. . . Ululu wa kubala pansi pa aneneri amenewo, bwanji, iwo pokhala Mawu, iwo analozera ku chidzalo cha iwoeni, chidzalo cha Mawu. Ndipo kenako potsiriza machitidwewo anafa, mpaka, "Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu."

118 Taonani momwe izo zinawonetsedwera mwa Yakobo. Taonani momwe izo zinawonetsedwera mwa Yosefe, ndendende. Wokondedwa ndi ake aba-. . . bambo ake; wodedwa ndi m'bale wake, popanda chifukwa. Iye anali wauzimu, amakhoza kulosera zinthu, ndi kutanthauzira maloto. Iye sakanatha kudziletsa kukhala chimenecho. Iye anangobadwa chomwecho. Iye anakonzedweratu kuti adzakhale chimenecho. Koma, ankadedwa ndi abale ake, ndipo potsiriza anamugulitsa iye mtengo wa zidutswa sarte za siliva, pafupifupi zidutswa sarte. Ndipo anakwezedwa mmwamba, anadzakhala pa dzanja lamanja la Farao. Penyani, mu ndende yake, munali wopereka chikho ndi wophika mkate; wina anatayika ndipo wina anapulumutsidwa.

119 Yesu mu ndende Yake, pa mtanda; wina anatayika, wina anapulumutsidwa. Ndendende. Ndipo kenako anakwezedwa mmiyamba ndipo anadzakhala pansi pa Mpando wachifumu wa Mulungu. Ndipo pamene Iye adzachokanso, padzamveka phokoso limene liti lidzamveke, "Pindani bondo," ndipo lirime lirilonse kuvomereza.

120 Ndipo pamene Yosefe anachoka pa mpando wachifumu ndi kuyamba kuyenda, lipenga linalira, ndipo bondo lirilonse linkayenera kugwada. "Yosefe anali akubwera."

121 Chotero, tsiku lina Lipenga lalikulu la Mulungu lidzawomba, akufa mwa Khristu adzawuka, ndipo bondo lirilonse lidzagwada, ndipo lirime lirilonse lidzavomereza kwa Mawu awa. Koma kodi Iye akutsatira chiyani? Kodi Iye akudzera chiyani kuno?

122 Zindikirani, iye anabweretsa Mawu athunthu awa amene anasandulika thupi, pansi pa ululu wa kubala wa aneneri amene anafuula, "Iye akubwera! Iye akubwera! Iye akubwera!"

123 Tsopano, koma iye anali wopanda mneneri kwa zaka foro handirede, molingana ndi mbiriyakale ndi Lemba, kuchokera kwa Malaki mpaka Yohane. Iwo ankangokhala ndi afioloje, ansembe, azibusa. Tsopano apa ife tikhoza kulingalira, popanda zimenezo, ndi mtundu wanji wa chikhalidwe chovunda umene kachitidwe kake kakuyenera kuti analimo, zaka foro handirede wopanda Uthenga wolunjika, wa PAKUTI ATERO AMBUYE, wochokera kwa Mulungu. Chotero, ansembe, aneneri, ndi ena otero, anali atazilowetsa izo mu nyansi zowopsya. Iye anali atavunda.

124 Kenako Yohane, Eliya wolonjezedwa wa Malaki 3, osati Malaki 4. Malaki 3, chifukwa Yesu ananena chinthu chomwecho mu—mu Mateyu mutu wa 11.

125 Pamene diso la mphungu la Yohane linajambulidwa, monga ndikukhulupirira momwe amafotokozera la Pember *Mibadwo Yoyambirira*, ndipo iye anati, "Pitani mukamufunse Iye ngati Iye ali Ameneyo, kapena tiyang'anire wina." Mukuona?

126 Ndipo Iye anati, Yesu, atawabwenza ophunzira ake, atawauza iwo kuti akhale pa msonkhanowo ndi kuwona chimene chitachitike. "Ndipo pitani, mukamuwonetse Yohane zinthu izi. Ndipo wodala ndi iye amene sakhumudwa."

127 Iye anatembenuka ndipo anayang'ana kwa ophunzira Ake ndi anthu amene Iye ankayankhula nawo. Iye anati, "Inu munapita kukawona chiyani pamene munapita kukamuwona Yohane?" Iye anati, "Kodi munapita kukawona mwamuna wovala zofewa?" Ndipo Iye anati, "Ine ndinena kwa inu, umenewo ndi mtundu umene umakhala m'nyumba za mafumu." Iye anati, "Kodi inu munapita kukawona a—a—bango limene limagwedezeka ndi mphepo?"

128 Mwa kuyankhula kwina, kanthu kakang'ono kalikonse kamene kamabwera, iye amagwedezeka nako? "Ine ndikukuuzani inu, ngati mungangobwera ndi kudzajowina gulu lathu, ife tikhoza kukupatsani malipiro abwinoko." Osati Yohane. "Ngati inu simungalalikire motsutsa *ichi* ndi *icho*, chabwino, mutha kujowina mmagulu athu." Osati Yohane.

129 Anati, "Ndiye inu munapita kukawona chiyani, mneneri? Ndipo ndinena ndi inu, woposa mneneri. Pakuti ngati inu mungathe kulandira izo, uyu ndi iye amene ananenedwa ndi mneneri, kuti, 'Ndidzatumiza mthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yanga, kuti akakonze njira.'" Ameneyo ndi Malaki 3:1.

130 Osati Malaki 4, nkomwe. Izo ndi zosiyana. Chifukwa, Eliya ameneyo akadzabwera, dziko likuyenera kuti lidzawotchedwa nthawiyomweyo, ndipo olungama adzayenda pa maphulusa a oyipa.

131 Tsopano zindikirani. Uthenga wake sunawakondoweze iwo mochuluka kuchokera ku tulo tawo tachipembedzo. Iwo

anangoti, "Kuli munthu wopenga kumusi uko. Kumudutsa iye, posakhalitsa. Akudzitcha yekha wopenga; iye akuyesera kumawamiza anthu kumusi uko mmadzi. Mukuona? Bwanji palibe chirichonse kwa mwamuna wokalamba ameneyo. Bwanji, iye sanavale ngakhale mtundu wa zovala zoyenera. Iye wavala chikopa cha nkhosa chitakulungidwa momuzungulira iye. Chabwino, iye ndi wosauka ngati nkhukutembo ya Yobu. Bwanji, ndi seminare iti imene iye anachokerako? Khadi la chiyanjano chanji? Ife sitigwirizana naye nkomwe mu misonkhano yake. Ife tidzangomulola iye kuti akhale pansi pamenepo ndikudzipha ndi njala." Mukuona? Dziko silinasinthe kwambiri, komanso machitidwe. Uh-huh. "Koma tidzangomusiya iye akhale pansi pamenepo. Iye alibe chirichonse . . . "

132 Inu mukudziwa chifukwa chimene iye sanatero? Kumbukirani, abambo ake anali ansembe. Koma nchifukwa chiyani iye sanatsatire mzere wa abambo ake, chimene chinali mwambo wake kuti ana achite mmasiku amenewo? Chifukwa iye anali ndi chinachake, Uthenga waukulu kwambiri. Iye anali woti adzamuwonetsera Mesiya, pakuti Mzimu Woyera unali utanena chomwecho. Wotsalira wamng'ono uja yemwe anali atabweretsedwanso ndi Uthenga wa Gabrieli, kumusi uko, ankadziwa kuti izo zikanadzakhala chomwecho. Chotero ife timauzidwa kuti, pafupifupi usinkhu wa zaka naini, iye anapita ku chipululu. Atataya abambo ake ndi amayi, kuti iye anapita mchipululu, chifukwa iye ankayenera kuti azikamva ndendende.

133 Chifukwa, mu nyumba yopambana ya fioloje kumeneko, iwo akanati, "Tsopano, ine ndikudziwa kuti iwe ukuyenera kukhala amene udzamlengeze Mesiya. Yesaya anati iwe ukubwera, chotero iwe udzakhala liwu limenelo. Tsopano, kodi iwe sukuganiza kuti M'bale Jones pano akungokwanirana nazo zimenezo ndendende basi?" Ndipo iye adzanyengereredwa mophweka.

134 Koma iye sanaphunzire kalikonse ka machitidwe awo. Uthenga wake unali wofunikira kwambiri. Iye anapita mchipululu, kuti akakhale.

135 Zindikirani. Uthenga Wake sunali ngati wa fioloje. Iye ankagwiritsa ntchito zoyimira. Iye anati, "Oh, inu m'badwo wa njoka." Kuwatchula azibusa amenewo, "njoka." Ichi, chimodzi mwa zinthu zoyipa zimene iye anazipeza mchipululu, chimodzi mwa zinthu zozembera, chinali njoka. Ndipo iye anaganiza, "Uko ndi kufananizira kopambana kumene ine ndikukudziwa." Iye anati, "Inu m'badwo wa njoka, ndani wakuchenjezani inu kuti muthawe mkwiyo ulinkudza? Musayambe kunena kuti, 'Ndife a *ichi* ndi *icho*,' pakuti Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kuwukitsa ana kwa Abrahamu." "Miyala iyi," chimene iye anachipeza mchipululu ndi m'mphepete mwa mtsinje.

136 "Komanso nkhwangwa," imene iye ankagwiritsa ntchito m'chipululu, "yayikidwa pa muzu wa mtengo," imene iye anaiwona m'chipululu. "Mtengo uliwonse umene sumabala chipatso chabwino," iye amadziwa kumene ankatenga nkhuni zake, mwaona, "umadulidwa ndi kuponyedwa pa moto," kupanga nkhuni kuchokera mwa iwo. Mukuona? Uthenga Wake sunali wa m'busa, nkomwe. Iwo unali wa chirengedwe, mu chipululu.

137 Koma iye anali ndi Uthenga woti awulengeze, ndipo anali ndi chikhulupiriro mu Uthenga wake, kunena kuti, "Mesiya ameneyo, wayandikira kwambiri kubwera, mpaka Iye ali pomwe pano pakati panu tsopano. Ine ndinena ndi inu, alipo Mmodzi wayima pakati panu, amene inu simukumudziwa, amene nsapato Zake sindiri woyenera kuzinyamula. Iye adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi Moto."

"Kodi Iye ndi ndani, Yohane?"

"Ine sindikudziwa."

138 Koma tsiku lina, kunabwera Mnyamata akuyenda kupita ku mtsinje, Mwamuna wowoneka mwawamba. Basi mu a. . . Yohane M'batizi wakale anali atayima pamenepo, mneneri wokalamba wodala, ndipo iye anayang'ana kutsidya la Yordano. Iye anati, "Taonani, apo pali Mwanawankhosa wa Mulungu amene akuchotsa tchimo la dziko lapansi."

"Iwe ukumudziwa bwanji Iye, Yohane?"

139 "Iye m'chipululu, amene anandiuza ine kuti ndipite kukabatiza m'madzi, anati, 'Pa Amene iwe udzawona Mzimu ukutsikirapo, Iye ndi Mmodzi amene ati azidzabatiza ndi Mzimu Woyera.'"

140 Uthenga Wake sukanabwera kuchokera ku kayimidwe ka zaumulungu kapena kachikhulupiriro kena kopangidwa ndi munthu. Iwo unkayenera kubwera molunjika kuchokera kwa Mulungu.

141 Pakuti, Uthenga wake sunawagwedeze iwo mochuluka kwambiri. Iwo ankaganiza, "Oh, iye anati iye anachiwona Icho. Ine ndikukaikira izo kwambiri. Ine sindinawone kalikonse. Ine ndinayang'ana. Oh, mai! Ine sindinawone kalikonse za izo," ansembe ndi iwo anatero.

142 Koma iye anawona Icho, ndipo ife tikudziwa tsopano iye anawona Icho. Ndithudi, iye anatero. Koma inu mukuzindikira chimene icho chinali nacho?

143 Icho sichinawakondoweze iwo kuwachotsa ku tulo tawo. Iwo anapitirirabe, kudula mutu wake, chimodzimodzi basi. Koma izo—izo sizinawakondoweze iwo konse.

144 Koma izo zinawatenga otsalirawo, iwo amene anali nawo Moyo mwa iwo, gulu laling'ono lija, Ana ndi—ndi Simeoni, ndi ochepa a iwo amene ankayembekezera onse Kudza kwa Ambuye.

Ndipo Ana, ali mu kachisi, wakhungu, mneneri wamkazi amene ankawatumikira Ambuye mwa mapemphero. Ndipo kenako tsiku lina pamene iye anali mu Mzimu . . .

145 Ndipo Simioni ananenera ndipo anati, mwamuna wokalamba, iye anati, "Mzimu Woyera ine unandiuza kuti sindidzawona imfa mpaka nditawona Khristu wa Ambuye."

146 Bwanji, ena a ansembe, inu mukudziwa, anati, "Munthu wachikulire wosauka, iye wangopenga pang'ono, inu mukudziwa. Bwanji, iye ali phazi limodzi mmanda tsopano, ndipo linalo likuterereka. Bwanji, ingomusiyani iye yekha. Iye wakhala ali mwamuna wokalamba wolemekezeka. Koma iye ali ngati . . . "

147 Koma, inu mukuona, kodi iye anali ndi chiyani? Izo zinawululidwa kwa iye mwa Mzimu Woyera.

148 Ndicho chinthu chomwe chomwecho chimene chawululidwa kwa anthu inu madzulo ano. Mzimu Woyera wakubweretsani inu pano pa chifukwa china. China . . . Mzimu Woyera! Tayang'anani pa ansembe awa ndi azibusa apa ochokera ku Methodisti, Baptisti, Katolika, ndi onse. Iwo anasunthidwa ndi Mzimu Woyera. Ora liri pano. Chotero Mzimu Woyera unasunthira pa iwo, ndipo iwo akhala akuwufunafuna Iwo, akuwuchitira njala. Kenako, basi mu a . . .

149 Tsiku lina, inu mukudziwa, analibe televizioni. Tithokoze Ambuye chifukwa cha tsiku limenelo.

150 Chotero, iwo, iwo anali kumusi ku mapiri a Yudeya. Kunali a—Mwana anabadwa. Nyenyezi inawonekera, ndi zina zotero.

151 Koma atatha masiku eyiti, amayiwo anamubweretsa Mwana wamng'onoyo, atakulungidwa mu nsalu yapa goli. Ndi nsalu yapa goli. Ine ndinena . . . ndinati izo zinali . . . Iwo analibe kanthu koti avale. Kanali a—kasanza kakang'ono kochokera pa goli la ng'ombe, ine ndinawuzidwa, iyo inali nsalu Yake yapa goli. Apa pakubwera Yosefe ndi iwo, akubwera umo ndi Mwana wamng'ono uyu.

152 Ine ndingalingalire amayi anayima chapatali, ndi ana awo aang'ono ali ndi zoluka ndi chirichonse. Anati, "Yang'anani pamenepo. Mukuona? Mukuona? Ndi uyo apo. Mukuona? Iye anali ndi pakati pa mwamuna ameneyo. Apa akubwera. Kuti, mutalikirane ndi iye. Khalani kutali." Iwo akuganizabe chinthu chomwecho.

153 Koma, Mariya, ali ndi Mwana ameneyo mmanja mwake, izo sizinapange kusiyana kulikonse chimene iwo ankaganiza. Iye ankadziwa kuti ameneyo anali Mwana wa Ndani.

154 Ndi momwemonso wokhulupirira aliyense amene amavomereza Mawu a Mulungu mu mtima mwawo! Sindikusamala chimene kachitidweko kakunena. Inu mukudziwa chimene Iwo ali. Ndi lonjezo la Mulungu. Iwo

anawululidwa kwa inu ndi Mzimu Woyera, pamene inu munaphimbidwa ndi Mphamvu Yake. Inu mukudziwa kumene Iwo ali. Palibe munthu ali ndi ufulu wolalikira Uthenga mpaka iye atakomana ndi Mulungu kuseri kwa chipululu mu chitsamba choyaka chimenecho, kumene kulibe kachitidwe kachipembedzo mdziko kangakhoze kuwafotokozera Iwo mophotchoera kwa inu. Inu munali kumeneko. Izo zinachitika kwa inu. Sindikusamala zomwe kachitidwe kakunena. Inu ndi mboni ya izo. Aleluya! Ine ndikumverera ngati munthu wachikuda wokalamba amene ine ndinkamukamba, "Ndiribe malo pano tsopano." Mukuona? Ine ndikumverera mwachipembedzo kwambiri pa nthawi ino, pamene ine ndikuganiza. Ndipo izo nzoona. Mulungu, Iyemwini, woululidwa kwa inu.

155 Simioni anali ndi lonjezo. Atakhala mowerengera mwake mmawa umenewo, oh, ine ndikuganiza pakhoza kukhala kuti panali ana mahandirede angapo amene ankabweretsedwa, mmawa uliwonse. Pafupifupi Ayuda mamillioni awiri ndi theka mdziko, ndipo ana awa amabwera mmenemo, ndipo ambiri amabadwa. Masiku eyiti aliwonse amayi ankayenera kubwera, kudzapereka nsembe ya chiyeretso. Ndipo tsopano apa pakubwera . . . Simioni, atakhala pamenepo, inu mukudziwa, mwinamwake akuwerenga mpukutu wa Yesaya. Ine sindikudziwa. Koma zonse mwa kamodzi . . .

156 Tsopano, ngati Mzimu Woyera wakupangirani inu lonjezo, Mzimu Woyera ukuyenera kusunga lonjezo limenelo, ngati Iwo ulidi Mulungu. Iye, ngati Iye . . .

157 Ngati munthu abwera ndi kudzanena chinthu chinachake, Mulungu osachiikira kumbuyo icho, icho si Lemba, kuyamba ndi kuyamba. Chiiwaleni chimenecho. Ndipo ngati iye anena kuti ziri choncho, ndipo Mulungu osachiikira kumbuyo icho, icho chikadali cholakwikabe.

158 Chifukwa, Mulungu amatanthauzira Uthenga Wake. Iye ndi wodzitanthauzira Yekha. Chimene iye amanena chimadzachitika, kenako Mulungu anati, "Mumvereni iye, pakuti icho ndi Choonadi." Izo ndi kuganiza kwa wamba chabe. Ngati iye anena kuti izo zichitika, ndipo izo nkuchitika, izo zikunena izo. Izo zikuyenera kukhala nthawi iliyonse, ndendende Choonadi, chifukwa Mulungu samanena mabodza.

159 Ndipo chotero ndiye apa pali Simioni wakhala pamenepo, akulolera kuzunzidwa. Iye anali wotsalira. Iye anali atamumva Yohane, ndi wotsalira wamng'ono wa tsiku limenelo. Ndipo apa iye anali atakhala pamenepo, akumvetsera pa mpukutu uwu, akudziwa. Ine ndikutanthauza, akudziwa kuti Yohane anali akubwera, chifukwa iye—iye anali gawo la wotsalira. Mawu anawululidwa kwa iye. Ndipo zonse mwakamodzi, pamene Mwana ameneyo anabwera mu kachisi, ndiye inali ntchito ya Mzimu Woyera kuwulula kuti Iye anali mmenemo. Chotero

iye, mosunthidwa ndi Mzimu, anatuluka kuchokera mchipinda chaching'ono chowerengeracho, anatsika kumene kudutsa mu holoyo, anagunda mzere uwo wa akazi. Akubwera mmusi motsatira mzere umenewo wa akazi mpaka iye anakafika pamene Mwana wamng'ono uyu anali, iwo onse anakhala kutali naye. Anamuyangata Mwanayo mmikono mwake, anati, "Ambuye, mulole wantchito Wanu apite mu mtendere, pakuti maso anga awona chipulumutso Chanu."

160 Ndipo pa nthawi imeneyo, mmodzi wina wa osankhidwa aang'ono mu tsiku limenelo, anali Anna, mneneri wamkazi. Iye anali atakhala pamenepo, wakhungu, pa kona. Anadzuka, wakhungu. Apa iye akubwera, motsogozedwa ndi Mzimu, pakati pa akazi onse ndi anthu akukhamukira mkati ndi kunja kwa kachisi, mpaka iye anabwera molunjika kumene Khristu Mwanayo anali.

161 Ngati Mzimu Woyera ukanakhoza kumutsogolera mkazi wakhungu kwa Iye, nanga bwanji gulu la Chipentekoste limene mukuyenera kukhala ndi kupenya kwanu? Ine sindipita patsogolo kenanso. Inu mukudziwa, kuyambira pamenepo. Zindikirani. Oh, mai! Momwe kuti mpingo umenewo ukuyenera kuti unali mu chisokonezeko chowopsya kachiwiri, iwo ndithudi ukuyenera kuti unali, mu tsiku limenelo! Koma izo zinagwedeza otsalira apang'ono, monga ine ndinanenera.

162 Tsopano tiyeni tikhale owona mtima. Ngati ife tikuwona mpingo umenewo uli mu chikhalidwe chimenecho lero, kodi ife sitinafike pa nthawi imeneyo panonso? Tsopano tangoyang'anani pa zinthu za lonjezo, za Baibulo, zomwe zikanadzakhala zikuchitika mu mpingo pa nthawi ino. Ife tikuwona zomwe zikuchitika mdziko, ndipo tikuwona kuti ilo liri kumapeto ake. Tsopano tiyeni tiyang'ane mu mpingo.

163 Iwo, mpingo, unali ndi ululu wa kubala pansi pa Luther. Tsopano, ife tikudziwa kuti pali mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, ndi atumiki asanu ndi awiri a mibadwo ya mpingo imeneyo, malingana ndi Chivumbulutso. Tsopano, pamene Luther ankayenera kuti abwere, izo ndithudi zinaponyera mpingo mu ululu wa kubala, koma izo zinamubweretsapo Luther. Uko nkulondola.

164 Zitachitika zimenezo, iwo unalowa mu vuto kachiwiri, kotero iwo unabweretsapo Wesley. Uko nkulondola.

Unabweranso kachiwiri, ndipo iwo unabweretsapo Pentekoste.

165 Aliyense wa iwo atumiki a m'badwo wawo, ankagwedeza . . . kubwerera ku Mawu, Uthenga wa m'badwo wawo, Uthenga wa molingana ndi Baibulo. Ine ndiri nalo likubwera, bukhu, pa izo, ndemanga ya mitu foro yoyambirira ya Chivumbulutso. Mudzawerenge ilo, mwamsanga pamene ife tidzalisindikiza ilo. Ndipo izo zikutsimikizira, mopanda mthunzi wa kukayikira,

chimene uthenga wa Luther unali, kulungamitsidwa; chimene kuyeretsedwa kuli, kachitidwe kotsatira mu kubadwa kwachirengedwe. Ndipo kenako panadzabwera achipentekoste, ndendende.

166 Tsopano, zindikirani, m'badwo uliwonse unkagwedeza mpingo ndi kuwupatsa iwo ululu wa kubala. Koma kodi iwo ankachita chiyani? Utabwera ululu wa kubala, mmalo mopitirira ndi Mawu, iwo anapeza gulu la amuna pamodzi monga momwe anachitira woyamba. Ndizo ndendende. Kutangochitika kugwedezeka kwa atumwi, ndiye ife tikuwupeza iwo ukuchokanso. Ndiye ife tikupeza, motsatira panadza ambiri a enawo, Agabasi ndi ambiri a okonzanso aakulu mmbuyo pachiyambi. M'badwo uliwonse unali utachita, pamene inu mukuwerenga Pre-Nicaea Council, Nicaea Fathers, ndi zonse mmbuyo. Inu muzipeza izo zonse mmenemo. M'badwo uliwonse unkagwedezeka, nthawi iliyonse mtumiki akabwera ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

167 Tsopano iwo uli mu siteji yoyipitsitsa, imene, molingana ndi Lemba, imene iwo sunayambe wakhalapo. Ife tiri mu m'badwo wa mpingo wa Laodikaya, "M'badwo, wa mpingo wolemera, umene sukudziwa izo."

168 Munalibe paliponse mu Baibulo pamene Khristu anaikidwapo kunja kwa mpingo, koma m'badwo wa Laodikaya. Iwo uli mu m'badwo woyipa kwambiri. Iwo ndi wovunda kwambiri umene unakhalapo. Anati, "Ine ndakhala ngati mfumukazi, osasowa kanthu."

169 "Ndipo simukudziwa kuti ndinu amaliseche, omvetsa chisoni, akhungu, osauka, ndipo osadziwa izo." Inde, bwana. Anati, "Ndikulangizani inu, bwerani mudzagule mankhwala a m'maso kwa Ine, kuti nditsegule maso anu." Ndipo izo zidza—izo ndithudi . . . Mankhwala a mmaso a Mulungu ndithudi adzabweretsa Kuwala kwa mpingo ngati iwo ukufuna kutsegula maso ake ku chimene Mulungu wanena.

170 Zindikirani, mwamsanga tsopano. Tsopano, iwo uli mu siteji imeneyo, kupyola mthunzi wa kukayika. Ife tiri mu m'badwo wa mpingo wa Laodikaya.

171 Tsopano, mtumiki wake walonjezedwa, mu Malaki mutu wa 4. Iye analonjeza kuti adzachita zimenezo. Ndipo Uthenga ndi woti uwabweretsenso Mawu, kuwabwezeretsa anthu ku Mawu. Kubadwa kukuyenera kuti kudzakhalepo. Iwo ukuyenera kubadwa, mwa Kubadwa kwatsopano, kuchokera molingana ndi Malaki 4.

172 Mu dziko la mpingo lero, pali machitidwe awiri amene akugwira ntchito. Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni. Tsopano ndikufuna kuwona ngati muti munene "ameni" pa izi. Pali machitidwe awiri amene akugwira ntchito mu dziko la mpingo lero. Ine ndizichotsa izi paphewa langa, ndipo

kenako ndithana nazo. Ife tonse tikudziwa kuti amenewo ndi Mawu a Mulungu, ndi kachitidwe ka chipembedzo. Pali machitidwe awiri amene akugwira ntchito. Monga momwe iwo analiri, Yakobo ndi Esau; wina akufuna Mzimu, wina akufuna thupi. Ndipo icho ndi chiyani? Esau ndi Yakobo ankamenyana m'mimba mwa amayi, ngakhale mpaka pamene iwo ankabadwa. Ndi chomwechonso zipembedzo ndi Mawu, zikumenyana, wina kutsutsana ndi mzake. Iwo akhala ali, kuyambira pamene Luther anabweretsa kukonzanso koyamba. Ine ndikukhulupirira kuti izo ndi zophweka kuti mukhoza kuzimvetsa. Mukuona?

173 Amuna awa, ngati iwo atenga *Ichi* ndi kutuluka ndi Iwo, iwo akhoza kukapanga zomveka kwa Iwo, mwaona, kuti uwafikitse Iwo pa malo amene inu mungathe. Ine ndikungofuna kuyika Mbewu iyi, kenako ndikuyembekeza iwo ayipanga Iyo kubwera ku Moyo. Zindikirani. Mukuona?

174 Zakhala ziri chomwecho nthawizonse. Ndi chifukwa chake iye ali ndi ululu wa kubala, chifukwa muli ndewu mwa iye.

175 Apo pali Esau, munthu wa mdziko basi, wachipembedzo kwambiri. Ndipo, oh, iye ali bwino, munthu wabwino, woyera, wakhalidwe, monga momwe ine ndikudziwira, koma iye sakudziwa kalikonse za Ufulu wakubadwa umenewo. Iye anabadwa mwanjira imeneyo. Iye anawumbidwa mwanjira imeneyo.

176 Ndipo Yakobo, ine sindikusamala chimene iye ali, iye akufuna Ufulu wakubadwa umenewo. Iye ndi wauzimu.

177 Ndipo awiri amenewo, lero, ali mu mmimba mwa mpingo. Pali kachitidwe kakakulu kakuyesera kuti kapangidwe, kotchedwa World Council of Churches. Ndipo kuchokera mmimba ya mpingo mukubwera ana awiri. Inu mungosunga mawu anga. Dziko liri . . .

178 Mawu akuyenera kubala Mpingo wa Mkwatibwi wa Mawu. Mpingo ukuyenera kuwomboledwa kuchokera mwa iye, Mkwatibwi wa Khristu. Iwo amene anagona mu mibadwo yonse adzapanga Mkwatibwi ameneyo amene anatulukira pa Mawu kuti iwo atulukire, monga kuchokera kumapazi mpaka kumutu kwanu. Iye amakhala—amakula, ndi zochuluka zimene inu mukuyenera kukhala nazo, ndi zina zotero. Pamene thupi likukula, momwemonso Thupi la Khristu limakula. Ndipo kenako potsiriza Mutu udzabwera kwa Iwo, Mutu wa Iwo udzatero, tsopano, ngati ife tingazindikire, chifukwa Ilo—Ilo lonse lalumikizana ndi Mutu. Mutu umachita kutembenukako, kukoka.

179 Koma machitidwe awa sadzakula kuchokera kwa Iwo, chifukwa iwo ndi kachitidwe, ndipo iko sikangakhoze kubala. Chisoso sichingathe kubala mulu wa tirigu. Koma zonse ziwiri ziri m'munda womwewo, kuthiririridwa ndi madzi omwewo, ndi

kuwala kwa dzuwa komweko. Chimodzi ndi Mawu; chimodzi si Mawu. Ndipo awiri amenewo akumenyana. Iwo akhala akumenyana kuyambira pa kukonzanso koyamba, ndipo iwo akumenyanabe.

180 Tsopano, ine sindikuyenera kupita patsogolo pa izo, ine nditero? Ndithudi inu mukudziwa chimene ine ndikunena. Inde, bwana. Ndi ife pamenepo. Ndi zimenezotu, kachitidwe. Kodi inu muli mu kachitidwe kotani?

181 Tangolingalirani tsopano, ngati inu mukanakhala mmbuyo mmasiku enawo, pansi pa kugwedeza kwa aneneri a Mulungu ndi Mawu amene ankabwera, ndi mbali iti imene inu mukanafuna kuti mukhale kumbuyo uko?

182 Chabwino, inu muli ndi kusankha komweko lero. Iye akukonzekera kuti abweretse Mawu angwiro kumbuyo uko, ndipo Mawu akubwerera Mkwatibwi wa Mawu. Monga a—mkazi ndi gawo la mwamuna, anatengedwa kuchokera kwa iye, kotero Mpingo udzayenera kukhala Mpingo wokhala mu Mawu, Mawu aliwonse a Baibulo; osati kachitidwe, mbalume, kapena popanda chowonjezera kwa Iwo. Iwo akuyenera adzakhale mu Mawu osayipitsidwa, angwiro, a unamwali. Kulondola.

183 Ndipo mmasiku a Kuwala kwa Luther, pamene mpingo unatseka, mphamvu ya Luther. Iwo unadutsa mu ululu, koma iye anabwera, "Olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro. Ndipo *uwu* si mgonero."

184 Tsopano, ife tikupeza, kuti, pansi pa masiku a John Wesley, iwo unapereka ululu kachiwiri, koma panali—apo panali Wesley amene anabadwa. Koma kodi iye anachita chiyani? Anabwereranso monga amayi anachitira.

185 Kenako pansi pa masiku a chipentekoste, abambo anu ndi amayi anatuluka mu chinthu chimenecho ndipo anachida icho. Iwo anapita pa msewu, amayi anu asanavale masitonkeni, akumenya chitini chakale, ndipo akuyankhula za ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi gitala ina yachikale. Iwo ankakhala kunja uko pa misewu ya magalimoto, ankakhala usiku wonse mu ndende. Ndipo ndife okhuthara kwambiri, ndipo tinabwerereranso mu bungwe ndipo tinadzipangira tokha matope omwewo, iwo anawakokera ana awo mkati, amene iwo anatulukamo. Iwo akanatembenuka mmanda awo. Iwo angachite manyazi ndi inu. Ine ndikudziwa kuti izo ndi zolimba, koma ndi Choonadi.

186 Inu mukuti, "Ine ndimaganiza kuti inu mumawakonda anthu." Ngati chikondi sichikonza, ndiye mungawonetsere bwanji chikondi? Chikondi chimakonza. Ndipo ndimalikonda dziko. . .ndine—ndine wachangu ndi mpingo wa Mulungu.

187 Ndipo kuwona machitidwe awa amene akuwumangirira iwo pansi pa mbalume, iwo ukuvunda. Ndipo Mulungu akulengeza

Mawu Ake kuti ndi Choonadi, ndipo iwo akugwiritsabe kwa iwo. Ameni. Uko nkulondola. Inu mukudziwa izo ndi zoona, m'bale, mlongo. Icho ndi Ichi basi. Imeneyo ndi njira yophweka yonenera Iwo. Uko—uko sikulongosola kwa Chigriki, ndi zinthu, koma ndi kulongosola ndi kusonyeza nzeru wamba. Ndithudi inu mukhoza kuwamvetsa Iwo. Thuu ndi thuu ndi foro. Mukuona? Tsopano ife tikudziwa kuti Iwo ndi olondola.

Tsopano, Mawu akuyenera kubala Mkwatibwi.

188 Koma kachitidwe kachikale kakuyenera kusunga mtundu wake. Iko kakuyenera kubala Esau amene anagulitsa ufulu wakubadwa wake.

189 Apa izo zikubwera. Ndikuzimverera izo. Ine ndikudalira kuti simukuganiza kuti ndine wamisala. Chabwino, ngati ine ndiri, ndisiyeni ine ndekha. Ine ndikumverera bwino chomwechi. Ine ndiri bwino mwanjira iyi kuposa momwe ndinaliri njira inayo. Ine—ine ndikhoza kukhala wopenga, kwa dziko. Ine—ine—ine ndikudziwa kumene ndiri. Ndikudziwa pamene ine ndaima.

190 Penyani. Iko kadzabala mwana wakufa, kachitidwe kachipembedzo kamene kati kadzabweretse zipembedzo zonse pamodzi, kuti kadzabale Esau amene amamuda Yakobo. Ameni. Ine ndikuyembekeza inu mukuziwona zimenezo, chobadwa chitafa, chipembedzo chakufa, onse a iwo akupita limodzi.

191 Oh, okhulupirira Mawu, gonjerani ku Uthenga wanga. Ndimvereni ine, osati Uthenga wanga, koma Uthenga Wake umene Iye akulengeza molimba kuti ndi Choonadi. Inu muyenera kusankha kuchokera kwinakwake. Inu simungakhale chete pambuyo pa izi. Inu mukuyenera kupanga chisankho chanu.

192 Mukukumbukira tsiku lina, ku Westward Ho uko, mmawa umenewo, pa kadzutsa uja, momwe Ambuye anandilola ine kuti ndikuwonetseni inu tirigu ameneyo? Momwe iye wakulira kudutsa Luther, kudutsa Wesley, ndi ngayaye, ndi zina zotero, ndi mphukira zazing'ono, mpingo uliwonse umayimiridwa mu phesi la chimanga. Kenako ndinapita mpaka mu tirigu uja, monga izo zinali, ndipo apo panali mankhusu aang'ono amenewo, ankawoneka chimodzimodzi basi monga njere yeniyeni ya tirigu. Pamene inu mupita kunja ndi kukawona, ngati inu simukumudziwa tirigu wanu, inu munganene kuti muli ndi tirigu pamenepo, koma ndi mankhusu chabe. Kenako inu mukatsegula mankhusu amenewo, mulibe tirigu mmenemo, nkomwe. M'mbuyo, pali mphukira yaying'ono ya moyo imene ikubwera. Inu mutenge galasi ndipo muyang'ane pa iyo. Ndipo pamene Pentekoste anatulukira koyamba, inali pafupi kwambiri, Yesu anati mu Mateyu 24:24, "Izo zikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka." Kodi icho

chinali choti chichite chiyani? Chothandizira kwa njere. Nkulondola uko? Tsopano, ngayaye . . .

193 Tayang'anani apa. Tsamba silimawoneka ngati njere imene inalowa, komanso ngayaye, koma iyo ndi yofanana pang'ono ndi imeneyo. Ndipo mankhusu amakhala ngati iyo mochuluka, komabe iwo si tirigu. Ndi chonyamulira tirigu.

194 Kodi inu simukuwona momwe mauthenga amenewo abwerera ndi ululu wa kubala? Koma Moyo unachoka pamenepo, kupita ku uthenga wotsatira. Moyo unatuluka kumene mwa Luther, kukalowa mu uthenga wa Wesley. Kuchoka mu uthenga wa Wesley, kupita mu uthenga wa chipentekoste. Tsopano ndi nthawi kachiwiri, kuti uchoke mu mankhusu. Vuto ndi chiyani? Pali chirengedwe, mmawonekedwe aliwonse, chikulengeza kuti icho ndi Choonadi.

195 Tsopano mukuwona chifukwa chimene inu mukuganiza kuti ndine wopenga. Mwinamwake ine ndiri, monga ine ndinanenera. Koma pali Chinachake mwa ine. Ine sindingathe kuchiletsa Icho. Ine sindinayike Icho pamenepo. Icho sichinabwere mwa kusankha kwanga komwe. Ndi Mulungu. Ndipo Iye amachitsimikizira Icho, kuti atsimikizire kuti Icho ndi Choonadi, kuchipanga Icho kukhala Choonadi. Osati monga ngati kuti ine ndiri ndi chirichonse chomutsutsa Luther, ndi Wesley, Achipentekoste, kapena Abaptisti, kapena aliyenseyo. Palibe chotsutsa aliyense. Kachitidweko ndi kamene ine ndikutsutsana nako, chifukwa Mawu amatsutsana nako; osati anthuwo. Tayang'anani pa ansembe awa ndi azibusa akhala pano, lero. Iwo sakanakhala pano ngati iwo akanamvetsera kwa kachitidweko, koma iwo anali ndi kulimba mtima kwa wamba, kwa Mawu a Mulungu, kuti atulukeko ndi kuwalandira Iwo. *Aleluya* amatanthauza "Mulungu wathu alemekezeke." Izo sizikupwetekani inu. Zimatanthauza "zikhale chomwecho." Ine ndikukhulupirira Icho. Ine ndikukhulupirira ndipo ndikudziwa kuti Icho ndi Choonadi. Icho chatsimikiziridwa kuti ndi Choonadi. Tsiku lina inu mudzazindikira, mwina mochedwa kwambiri. Tsopano penyani. Penyani.

196 Baibulo linati, "Mkazi Wake wadzikonzekeretsa Yekha," pa mapeto a m'badwo. Kodi Iye anadzikonzekeretsa Yekha chotani, kuti akhale Mkazi Wake? Ndipo kodi Iye amachita chiyani? Ndi chovala cha mtundu wanji chimene Iye anali atavala? Mawu Ake Omwe. Iye anali atavala mu Chirungamo Chake. Ndi chimenecho. Ndi zoona. Mukuona?

197 Masomphenya! Zindikirani, ndikungotseka tsopano. Ine ndikufuna kunena chinthu chimodzi ichi ndisanatseke. Ndi chimene chinandipangitsa ine kunena izi. Tsopano, ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Ngati munthu anganene zimenezo, popanda, kuziyika izo mu kuganiza kwake komwe, iye angakhale wachinyengo ndipo akuyenera kupita ku gehena chifukwa cha

izo. Uko nkulondola. Ngati iye angayesere kutenga gulu la anthu, anthu abwino monga awa, ndi kuwanyenga iwo, bwanji, iye angakhale mdierekezi mu thupi la munthu. Mulungu sangamulemekeze konse iye. Kodi inu mukuganiza kuti Mulungu angalemekeze mdierekezi kapena bodza? Zosatheka. Mukuona? Izo zimadutsa pamwamba pa mitu yawo, ndipo samazimvetsa izo. Iye amakokera kunja Osankhidwa.

198 Tayang'anani pa aneneri onse kudutsa mu m'badwo, momwe Iye ankapezera Osankhidwa.

199 Penyani, kubwera mmusi modutsa, ngakhale mpaka ku kukonzanso. Monga, mpingo wa Roma Katolika unamuwotcha Joan waku Arc pa nkhuni, chifukwa chokhala mfiti. Uko nkulondola. Kenako iwo anadzapeza kuti iye sanali. Iye anali woyera. Ndithudi, iwo anachita kudzitunduza, anakumba matupi a ansembe ndi kuwaponyera iwo mu mtsinje. Koma, inu mukudziwa, koma zimenezo sizithetsa izo m'mabuku a Mulungu. Ayi. Iwo anamutcha Patrick Woyera mmodzi, nayenso, inu mwaona, ndipo iye ali pafupifupi mochuluka monga ine ndiriri. Chotero, ife tikuzindikira, tayang'anani pa ana ake. Yang'anani pa malo ake, mmwamba, yang'anani pa angati amene anaphedwa. Yang'anani pa ofera ndi kuwona kuti ndi angati amene anaphedwa pamenepo. Inu muwona, sizinali chomwecho.

200 Koma zodzinenera za anthu, izo sizimapangitsa izo kukhala chomwecho. Ndi chimene Mulungu ananena ndi kutsimikizira, kuti ndi Choonadi. "Tsimikizirani zinthu zonse. Gwiritsitsani molimba chimene chiri chabwino."

201 Tsopano ife tikupeza, tsopano, kuno pafupifupi miyezi ingapo yapitayo, mmawa wina, ine ndinali ndikutuluka mnyumba, ndipo masomphenya anadzabwera.

202 Ndipo ndikutsutsa aliyense pano, amene amadziwa zaka zonsezi, kuti anene nthawi iliyonse imene Ambuye anandilola ine kunena "PAKUTI ATERO AMBUYE" koma zomwe zinachitika. Ndi angati akudziwa kuti ndi Choonadi? Kwezani dzanja lanu. Kulondola. Kodi aliyense angayankhule motsutsa? Izo ndi zoona.

203 Musapereke chidwi chirichonse kwa wa mthenga. Muziyang'ana pa Uthenga chimene uli. Icho ndi chimene chiri. Mukuona? Iwo suli choncho. Musamayang'ane zazing'ono . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . wadazi, inu mukudziwa, munthu, chifukwa ndi a—ndi munthu basi, tonse, ndipo ndife tonse ofanana. Koma muziyang'ana zimene zikuchitika. Izo ndi zimene zimalongosola izo. Ine ndinatengedwa . . .

204 Tsopano, ine ndikudziwa anthu amanena mitundu yonse ya zinthu, ndipo ife tikudziwa kuti zambiri si zolondola. Ine sindingathe kuyankha pa zomwe wina, munthu aliyense

anganene. Ine ndikuyenera kuyankha zomwe ine ndikunena. Ine ndikhoza kungonena ngati icho chiri Choonadi, kapena ayi. Ndipo ine—ine—ine ndi amene ndikuyenera kukhala oyankhira pa izo, osati zomwe wina akunena. Ine sindingamuweruze aliyense. Ine sindinatumidwe kuti ndidzaweruze, koma kuti ndidzalalikire Uthenga. Zindikirani.

205 Ndinkayenera kuti ndidzakhale ndi a—chiwonetsero cha Mpingo. Ndipo ine ndinatengedwa ndi Winawake Amene ine sindimakhoza kumuwona, ndipo ndinayikidwa, monga, poyimapo. Ndipo ine ndinamva nyimbo yokoma kwambiri imene ine ndinayamba ndaimvapo. Ndipo ine ndinayang'ana, akubwera, ndi gulu la madona aang'ono, pafupifupi, ankawoneka ngati, oh, usinkhu wina pafupifupi twente, eyitini, twente. Ndipo iwo onse anali ndi tsitsi lalitali, ndipo anali atavala madiresi osiyanasiyana, mtundu, madiresi. Ndipo iwo anali akuguba mwangwiro basi mu sitepe, ndi nyimbo imeneyo, monga izo zikanakhalira. Ndipo iwo anachoka kumanzere kwanga, akuzungulira njira *iyi*. Ndipo ine ndinawayang'ana iwo. Ndipo ine ndinayang'ana ndiye kuti ndiwone Amene amayankhula kwa ine, ndipo ine sindinkawona aliyense.

206 Kenako ndinamva gulu loyimba gwedemula likubwera. Ndipo pamene ine ndinayang'ana cha ku mbali yanga ya kumanja, akubwera kumtunda njira *iyi*, akubwerera, apa panadzabwera mipingo ya mdziko. Ndi ena a . . . Aliyense atanyamula mbendera yake, kuchokera kumene iwo ankachokera. Zina mwa zinthu zowoneka zauve zomwe ndinaziwonapo m'moyo wanga! Ndipo pamene mpingo wa Chiamerika unabwera, iwo unali woopsya umene ine ndinayamba ndawuwonapo. Atate Akumwamba ndi Woweruza wanga. Iwo anali atavala masiketi otuwa awa, monga ena a atsikana aku bara awa, opanda nsana pa iwo, pamwamba *apa*; atanyamula ngati chidutswa chotuwa cha pepala; ndipo ngati kuvina hula; penti; tsitsi lalifupi, lodulidwa; akusuta ndudu; ndipo akudzipotokola, pamene iwo ankayenda monga gwedemula.

Ndipo ine ndinati, "Kodi umenewo ndi mpingo wa United States?"

Ndipo Liwu linati, "Inde, ndi umenewo."

207 Ndipo pamene iwo ankadutsa, iwo ankayenera kugwira icho monga *chonchi*, ndi kuyika pepala kumbuyo kwawo pamene iwo ankadutsa pamenepo.

208 Ine—ine ndinayamba kulira. Ine—ine ndinangoganiza, "Mwa ntchito zanga zonse, ndi zonse zomwe ndachita." Ndipo chirichonse chimene ife atumiki tagwira ntchito limodzi . . . Ndipo, abale, ine—ine sindikudziwa kuti mungakhulupirire bwanji za masomphenya awa; koma ndi Choonadi, kwa ine. Nthawi zonse zatsimikiziridwa kukhala zoona. Pamene ine

ndinawona izo, ndi podziwa chimene chinali kuchitika, mtima wanga unasweka mwa ine. “Ine ndachita chiyani? Ine ndaphonya bwanji iwo? Ine ndakhala molondola ndi Mawu amenewo, Ambuye. Ndipo ine ndikanachita bwanji zimenezo?”

209 Ine ndinaganiza, “Bwanji Inu munandipatsa ine masomphenya, osati kale kwambiri, ndi kundiwona ine Mmenemo? Ndipo ine ndinati, ‘Chabwino, kodi iwo adzayenera kuweruzidwa?’ Iye anati, ‘Gulu la Paulo, nalonso.’ Ine ndinati, ‘Ine ndalalikira Mawu omwewo amene iye analalikira.’” Christian Business Men inalemba nkhani ya zimenezo. Ndipo ine ndinati, “Bwanji? Nchifukwa chiyani izo zikukhala chomwechi?”

210 Ine ndinawona gulu lija la mahule likudutsa monga choncho, onse atavala monga choncho, ndipo wotchedwa, “Mpingo wa Abiti U.S.A.” Ine ndinangokomoka.

211 Ndiye, molunjika, ine ndinamva nyimbo yokoma kwenikweni ija ikubwera kachiwiri, ndipo apa panadzabwera Mkwatibwi wamng’ono yemwe uja akudutsa kachiwiri. Iye anati, “Izi ndi zimene zikutulukira, ngakhalebe.” Ndipo pamene Iye anadutsa, Iye anali chimodzimodzi monga Iye anali pamalo oyambirira, akuyenda mwa sitepe ya nyimbo za Mawu a Mulungu, akuguba apa akudutsa. Ndipo pamene ine ndinawona izo, ine ndinaima pamenepo ndi manja onse awiri mmwamba, ndikulira, monga *choncho*. Pamene ndinadzafika, ine ndinali nditaima pa khonde langa kunja uko, ndikuyang’ana kunja komwe kutsidya kwa bwalo.

212 Chiyani? Iye akuyenera kukhala Mkwatibwi yemweyo, mtundu womwewo, womangidwa kuchokera ku zipangizo zamtundu womwewo zimene Iye anali poyambirira. Tsopano werengani Malaki 4 ndipo muwone ngati ife sitikuyenera kukhala ndi Uthenga mmasiku otsiriza, umene uti udza “tembenuze mitima ya ana kwa atate,” kubwerera ku Uthenga wa chipentekoste wapachiyambi, Mawu ndi Mawu. Abale, ife tiri pano.

213 Tsopano, mpingo uwu ukuyenera kukhala ndi chizindikiro, ndi chizindikiro chake chotsiriza. Ife tikupeza apa, mu—mu—mu Lemba, onani tsopano, onani, ululu wa kubala umene uli mu m’badwo wa Laodikaya uno. Iwo ndi wotopetsa. Mpingo wawo ukubadwanso mwatsopano. Osati . . .

214 Sipadzakhalanso bungwe lina. Aliyense amadziwa kuti nthawi iliyonse uthenga ukapita . . . Afunseni azambiri yakale awa. Uthenga ukapita, bungwe limatuluka kuchokera mwa iwo; oh, Alexander Campbell, china chirichonse, Martin Luther, ndi chirichonse. Iwo anapanga bungwe kuchokera mwa iwo. Ndipo kawirikawiri uthenga umangoyenda kwa pafupifupi zaka zitatu, chitsitsimutso. Uwu wakhala ukupita kwa zaka fifitini, ndipo

sipanakhale bungwe lochokera kwa iwo. Chifukwa chiyani? Mankhusu anali otsiriza. Ife tiri kumapeto.

215 Mukuona ululu wa kubala? Mukuona chimene chiri vuto? Otsalira okha adzatulutsidwa. Otsalira okha adzatulutsidwa. Ndipo ndi chifukwa chake ine ndikulira, ndi kulimbikira, ndi kukankha, ndi kusiya pambali kukondedwa kulikonse kwa munthu pa dziko, kuti apeze kukonderedwa ndi Mulungu, ndi kumangosunthira chitsogolo mu Mawu Ake.

216 Iwo ukumva ululu. Limenelo ndi limene liri vuto. Iwo ubala. Iwo ukuyenera kupanga kusankha kwake. Cholembedwacho chiri pakhoma. Tikuwona kuti dziko lapansi latsala pang'ono kupita. Uko nkulondola. Ndipo ife tikuwuwona mpingo, iwo wavunda kwambiri, iwo watsala pang'ono kuti upite. Ndipo ululu wa kubala uli pa izo zonse, pa dziko lonse ndi mpingo.

217 Ndipo patsala pang'ono kuti dziko latsopano libadwe, ndi Mpingo watsopano kuti ubadwe, kuti upite kwa iwo, kwa Zakachikwi. Ife tikudziwa zimenezo.

218 Tapenyani. Mulungu akuwupatsa iwo. . . Ndipo mvetserani kwa ichi mwatcheru, kenako ine ndikutseka. Chizindikiro chake chomaliza; Uthenga wake wotsiriza, chizindikiro chake chomaliza. Chizindikiro chake chotsiriza, ndi, iwo ukuyenera kulowa mu zikhalidwe monga iwo unali pachiyambi; dziko, mpingo.

219 Taonani momwe izo zinakhalira pachiyambi, zaka zonsezo, popanda, kuchokera kwa Malaki mpaka Yesu. Tayang'anani pa iwo, zaka zonsezo tsopano. Tayang'anani pa iwo, zonse kumbuyo uko, chivundi chimene iwo analowa mwa iwo. Tayang'anani pa dziko lapansi, momwe ilo limakhalira pa nthawi iliyonse, monga mmasiku a Nowa, zina zotero. Likuyenera kukhala mu mtundu womwewo wa choyimira, ndipo ife tikuziwona izo. "Monga zinkakhalira mmasiku a Nowa." Ife tikuziwona zinthu zonsezi zikungofanizira.

220 Kenako, ife titenga chizindikiro chimodzi chomaliza. Mu Luka, mutu wa 17, ndime ya 28, Yesu anati, "Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwecho izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu." Pakuti, monga izo zinali mu Sodomu, mwaona. Tsopano, Yesu ankawerenga Baibulo lomweli, Genesis yemweyi imene ife tikuwerenga. Tsopano, potseka, musaphonye izi. Baibulo lomwelo limene ife tikuwerenga, Yesu ankawerenga. Ndipo Iye anati kwa Mpingo Wake, "Yang'anani mmbuyo ndipo mukawone pamene masiku a Sodomu adzabwerererenso," anthu opotozedwa, amuna otaya chirengedwe chawo.

221 Tayang'anani pa ogonana amuna kapena akazi okhaokha, momwe achulukira padziko lonse lapansi lero, mu nyuzipepala posachedwapa. Inu mukuyenera mudzalowe mu ofesi yanga ndi kudzawerenga makalata ochokera kwa amayi, a anyamata awo. Ndipo kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha

kukuchulukirachulukira, ine ndikuganiza, ndi twente kapena sarte peresenti mu—mu California, yekha, chaka chatha. Gulu lalikulu la . . . la ngakhale anthu a m'boma, atsimikizira kuti ndi ogonana amuna kapena akazi okhaokha. Inu amuna a m'boma mukudziwa zimenezo. Magazini yanu, ndinaiwerenga iyo, ndipo mu zinthu zosiyanasiyana zachitika. Ngati inu . . .

222 [Mlongo akuyankhula mu lirime lina, ndipo kenako iye akupereka kutanthauzira. Mlongo yemweyo akuyankhulanso mu lirime lina, ndipo kenako akuperekanso kutanthauzira. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

223 Tsopano, ngati ine ndiri ndi kumvetsa kolondola, apa, kwa Lemba, ndizo ndendende zomwe Mulungu ananena kuti zikanadzachitika: "Mulole iye amene ayankhula lirime apempherenso kuti atanthauzire."

224 Izo ndi zoona. Ine ndakuuzani inu Choonadi, ndiye Mulungu ali pano, akutsimikizira Icho. Ndi Choonadi. Izo nzoona.

225 Tsopano tayang'anani. Kodi Uthenga wotsiriza uja umene Yesu ananena unali chiyani? "Monga zinali mmasiku a Sodomu," tsopano penyani, basi dziko la Amitundu lisanawotchedwe, moto. Tsopano yeserani kumvetsa. Chinachitika ndi chiyani? Panali gulu la anthu, mamembala ofunda a mpingo, monga Loti ndi gulu lake kumusi mu Sodomu. Uko kunali munthu wina amene anali atatuluka kale mmenemo. Iye sanali mmenemo, kuyamba ndi kuyamba. Ameneyo anali Abrahamu, mmodzi amene anali ndi lonjezo la mwana wakudza. Inu mukundimvetsa? Nenani, "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino.

226 Ndipo, tsopano, chimake cha chiwonongeko chisanafike, Mulungu anawonekera kwa Abrahamu mmawonekedwe ambiri, koma nthawi iyi Iye akuwonekera ngati Munthu. Iye anali Munthu. Ndipo iye anabwera kwa Mulungu.

Tsopano, inu mukuti, "Iye sanali Munthu."

227 Iye—iye—iye—iye anali Mulungu mwa Munthu. Abrahamu anamutcha Iye, "Elohim." Iye anali Munthu.

228 Ndipo, taonani, Iye anadzakhala pansi, atatembenuzira nsana Wake ku hema, ndipo Iye anati, "Ali kuti Sarah, mkazi wako?"

Anati, "Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu."

229 Anati, "Ndidzakuchezerani inu molingana ndi nthawi ya moyo, imene ndinakulonjezani inu." Ndipo Sarah anaseka. Ndipo Iye anati, "Nchifukwa chiyani Sarah waseka?" Mukuona?

230 Tsopano, izo ndi zomwe zinkachitika mu tsiku limenelo. Kungosonyeza chizindikiro chotsiriza chimene Abrahamu anachiwona, gulu Losankhidwa linatulukira, kutali ndi Sodomu. Tsopano, musaphonye fanizo ili, chirichonse chimene

inu mungachite. Gulu limene linali litatulutsidwa, limene silinali mu Sodomu, kuyamba ndi kuyamba.

231 Koma awiri a Angelowo anapita kumusi ku Sodomu. Ndipo pamene Iwo anakafika kumusi kumeneko, ife tikumupeza Loti. Ndipo Iye anamupeza iye mu chikhalidwe chobwerera mmbuyo, onse ogonana amuna kapena akazi okhaokha ndi zosokoneza. Inu mukuidziwa nkhaniyo.

Koma pali Mmodzi amene anatsalira ndi Abrahamu, anali Elohim.

232 Iwo analalikira Mawu kumusi kumeneko. Kulalikira Mawu kunawakantha iwo khungu, ndipo iwo sanathe kulipeza khomo. Icho ndi chimene chiri lero.

233 Koma Iye amene anatsala ndi gulu limene linatulutsidwa, anachita chozizwitsa pamaso pa Abrahamu, kuti awonetsere Chimene Iye anali, ndipo anali ndi Abrahamu.

234 Iye anati, “Nchifukwa chiyani Sarah waseka?” zokhuza mwana uyu. Ndipo Sarah anabwera ndipo anati iye sanatero. Ndipo anati, “Koma iwe unatero.” Ndipo Iye akanamupha iye pomwe apo ngati iye akanati asakhale gawo la Abrahamu.

235 Momwemonso Mulungu akanatipha ife ngati ife tikanati tisakhale gawo la Khristu. Chifundo cha Khristu chonse chimatigwirizanitsa ife pamodzi, ife okayikira ndi opotoza mu Mawu.

236 Koma, zindikirani, zindikirani zomwe zinachitika. Yesu akutembenuka tsopano, ndipo akuti, “Monga mmene zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala mu nthawi yotsiriza pamene Mwana wa munthu adzayamba kudziulula Yekha.” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Mukuona? “Mwana wa munthu” nthawizonse, mu Baibulo, ndi *mneneri*. Mukuona? Iye anabwera mu dzina la ana atatu: Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu, Mwana wa Davide. Mukuona? Ndipo Iye anatchula Dzina Lake, “Mwana wa munthu,” chifukwa imeneyo ndi ntchito imene Iye anayichita, ya mneneri, mpenyi. Iye anati, “Mmasiku monga zinakhalira a Nowa, pamene Mwana wa munthu adzayamba kudziulula Yekha, imeneyo idzakhala nthawi ya chimaliziro.”

237 Tsopano tiyeni tingoganiza, kwa miniti yokha. Dziko silinayambe lakhalapo ndi mtumiki pa dziko lapansi. Ife takhalapo ndi Finney, Sankey’s, Moody’s, Finney’s, Knox, Calvin, ena otero, onse kuzungulira dziko, atumiki kwa mpingo mu ululu wa kubala uwu. Koma sitinakhalepo ndi mwamuna amene amapita ndi uthenga wapadziko lonse, mpaka lero, wa dzina lake lothera ndi h-a-m. A-b-r-a-h-a-m, amene ali zilembo sikisi . . . A-b-r-a-h-a-m ndi zilembo seveni.

238 Ife tiri naye mmodzi lero wotchedwa G-r-a-h-a-m, zilembo sikisi, ndipo sikisi ndi nambala ya dziko, tsiku lachirengedwe.

Ndi liti limene dziko linayamba lakhalapo ndi munthu kumusi kwa ilo tsopano, akulalikira kumusi mu *kosmos*, kumusi uko mdziko, kumusi uko akuyitana anthu kuti atuluke, "Lapani, lapani! Muwonongeka, kapena tulukanimo," kufikira m'badwo uno? G-r-a-h-a-m, taonani zimene iye akuchita, akulalikira Mawu, akuchititsa khungu akunja, akuyitana, "Tulukani," mtumiki wochokera kwa Mulungu. Yesu ananena kuti izo zidzachitika pamene Mwana wa munthu adzadziulula Yekha. Tsopano, izo, izo ziri kuti? Kunja uko mu dongosolo la mpingo, dziko. Ndipo iwo anayamba kumuda munthuyo, chifukwa cha zimenezo.

239 Koma, kumbukirani, panali gulu, aponso, limene linali gulu lauzimu, gulu la Yakobo, osati a—osati gulu la Esau. Panali gulu la Yakobo limene linkafunafuna mwana, amene sanali mu Babeloni ameneyo, ndipo iwo analandira Mtumiki. Mukumvetsa? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Abrahamu, A-b-r-a-h-a-m-u, iwo anamulandira Mtumiki. Ndipo Mtumiki ameneyo, chinali chiyani chachikulucho, chinthu chapadera chimene Iye anachita, kuti awonetsere kuti icho chinali pa nthawi yotsiriza? Iye anazindikira maganizo amene anali mmalingaliro a Sarah.

240 Ndipo Yesu, Mwana wa Mulungu, amene anasandulika thupi, kuwonetsera kuti Mzimu wa Mulungu udzabwerera mu Gulu laling'ono losankhidwa ilo la mu nthawi yotsiriza, ndipo adzadziulula Yekha mwanjira yomweyo. Ululu wa kubala! Oh, m'bale, chonde yesetsani kuti mumvetse. Yesetsani mwamphamvu. Tsegulani mitima yanu miniti yokha. Muyang'ane kwa Khristu. Mulungu yemweyo ali pomwe pano tsopano. Mmodzi yemweyo. Iye analonjeza zinthu izi. Ndipo ngati Iye analonjeza izo, Iye ndithudi ndi wokhoza kuchita izo.

241 Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe. Ine ndikufuna kuti inu mungoganiza, mwaulemu.

242 Atate, izo ziri mmanja Mwanu tsopano. Ine ndachita zonse zomwe ndingathe. Ine ndikupemphera kuti Inu muwathandize anthu ku—kuti amvetsetse. Mbewu yabzalidwa. Thirani madziwo, Mzimu, pa Iwo, Ambuye, ndi kuwathirira Iwo kwa ulemelero Wanu. Ngati ine ndalakwitsa, Ambuye, ine sindimatanthauza kutero. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti—kuti Inu mutanthauzire Iwo molondola, ku mitima yawo, kuti iwo akhoze kuwona ndi kumvetsa. Perekani izi, Ambuye. Mu Dzina la Yesu, ine ndikupemphera. Ameni.

243 Ambuye akudalitseni inu. Ine ndimakukondani inu. Mulungu uyu amene analalikira Mawu awa, Mulungu uyu amene ali ndi udindo pa Mawu awa. . .Ine ndiri ndi udindo wonena Izo. Iye ndi Mmodzi amene akuyenera kuwafulumizitsa Iwo. Mulungu yemweyo ali pano.

244 Tsopano, ndi angati kunja uko ali ndi chosowa? Kwezani dzanja lanu. Kodi Iye analonjeza kuti adzachita zinthu izi mmasiku otsiriza? Tsopano inu muyang'ane kwa ine. Tsopano ziri monga Petro ndi Yohane ananenera, "Muyang'ane pa ife." Monga ngati . . . Mukuona? Iye anamuuza iye. Tsopano inu muyang'ane mbali iyi. Tsopano, chonde musayendeyende. Izi ndi kwambiri . . . Ine ndi—ine ndikuyesetsa, mtima wanga wonse mkati mwanga. Mungokhala molemekeza kwenikweni. Mukuona? Aliyense wa inu, mzimu, pamene inu musuntha. Chifukwa, ndinu mmodzi. Ndipo ine ndikuyesetsa kuti ndigwire chikhulupiriro cha anthu.

245 Mkazi wamng'ono anadutsa ndipo anakhudza chovala Chake, anatuluka ndipo anakakhala pansi. Yesu anamuuza iye chimene mavuto ake anali, ndipo iye anachiritsidwa.

246 Ndipo tsopano Iye analonjeza kuti adzachita izo kachiwiri, Mwana wa munthu akanadzadziulula Yekha monga Iye anachitira ku Sodomu. Dziko liri mu chikhalidwe chimenecho. Mpingo uli mu chikhalidwe chimenecho. Tsopano kodi Mulungu wasunga Mawu Ake? Muone ngati Iye watero, kapena ayi. Oh, ife takhalapo nazo zizindikiro, kulumpha, kuyankhula mmalirime, ulosi, zina zotero. Koma, dikirani, pali chizindikiro china. Oh, ife tiri nazo zokopera zachithupi zambiri. Izo zimangopangitsa chenichenicho kuwala. Dola yabodza iliyonse imayenera kupangitsa yeniyeniyo kuwala.

247 Tsopano inu mupemphere. Inu mukhulupirire. Basi, ine—ine ndikukutsutsani inu kuti muchite zimenezo. Inu muyang'ane, ndipo mukhulupirire zimene ine ndakuuzani inu. Ndi angati akukhulupirira izi kuti ndi Choonadi? Musasamale yemwe inu muli, komwe inu muli. Ine basi . . .

248 Aliyense muno, momwe ine ndikudziwira, ndi mlendo kwathunthu, kupatula Bill Dauch ndi mkazi wake akhala pomwe pomwe, momwe ine ndikudziwira. Ine ndikuganiza ine ndikumudziwa mlaliki wamng'ono uyu apa wochokera ku Germany, wakhala apo. Ndi, m'bale, ndi anthu awiri kapena atatu akhala apo pomwe.

249 Winawake kumbuyo mwa omvetsera, taonani, kumbuyo komwe. Ine ndikukutsutsani inu kuti mukhulupirire zomwe ine ndakuuzani inu ndi Choonadi.

250 Nanga bwanji pamene Mngelo uja wa Ambuye anadzatsika pa mtsinje kutsidyako, zaka sarte-firii zapitazo, ndipo ananena ndemanga iyi? Ine ndinadziwa bwanji?

251 Ndipo abusa anga omwe a Baptisti ananditulutsa ine mu mpingo, anati, "Iwe—iwe unali ndi malubwelubwe, Billy."

252 Ine ndinati, "Malubwelubwe, palibe, Dr. Davis. Umo ndi momwe inu, momwe mumaziwonera, mukhozanso kungotenga khadi langa lachiyanjano."

253 Ine ndinkadziwa kuti padzakhala winawake, kwinakwake, akanati adzakhulupirire Izo. Mulungu sangatumize Uthenga pokhapokha patakhala wina woti awulandire Iwo.

254 Oh, ndithudi, pamene ine ndinapita kukapempherera odwala, izo zinali zabwino kwambiri. Koma pamene ine ndinayamba kukuuzani inu Choonadi cha Mawu, ndiye izo ndi zosiyana. Inu mukuyenera kudziwa. Uthenga uliwonse wakhala mwanjira imeneyo.

255 Yesu anali wodabwitsa pamene Iye ankapita mu mpingo ndi kumachiritsa anthu, ndi chirichonse. Koma pamene Iye anakhala pansi tsiku lina, ndipo anati, "Ine ndi Atate Anga ndi amodzi," oh, izo, izo zinachita izo. "Pokhapokha inu mutadya thupi la Mwana wa munthu, ndi kumwa Magazi Ake, inu mulibe Moyo mwa inu." Iye sanafotokoze Izo. Iye ankafuna kuti awone amene adzayime pafupi ndi Iye. Kulondola.

256 Inu mukuganiza bwanji, a—gulu la madokotala ndi zinthu, ndikuti, "Munthu ameneyo ndi. . .Bwanji, Iye ndi wakumwa magazi. Adye thupi Lake ndi kumwa Magazi Ake?" Iye sanazifotokoze Izo. Iye sanazifotokoze Izo.

257 Koma, komabe, Mawu amenewo anali akugwira, kwa atumwi amenewo. Iwo sanasamale. Iwo sanazimvetse Izo. Iwo ankakhulupirira Izo, mulimonse. Mukuona? Iwo ankadziwa, chifukwa iwo anali atawona ntchito za Mulungu, ndipo iwo ankadziwa kuti izo zinali. Iye anati, "Iwo ndi amene amachitira umboni za Ine."

258 Apa pali mwamuna, mkazi wakhala pomwe pano, wakweza dzanja lake mmwamba. Tsopano, inu mukhoza kunditcha ine wotentheka, ngati inu mukufuna kutero; koma Lawi la Moto lomwelo, limene linawatsogolera ana a Israeli kudutsa mchipululu, liri pa mkazi ameneyo.

259 Tsopano, kumbukirani, Yesu anati, "Kanthawi pang'ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine. Ine ndinachokera kwa Mulungu. Ine ndikupita kwa Mulungu," itachitika imfa Yake, kuyikidwa mmanda. Iye anawauza Ayuda. Iye anati, "Ine. . . "

260 Iye anali Thanthwe lija limene linali mchipululu. Iye anali Lawi la Moto lija, "INE NDINE AMENE INE NDIRI." Anali ndani "INE NDINE"? Lawi la Moto lija mu chitsamba choyaka chija. Ndi kulondola uko? Ndipo Iye anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Anati, "Ine ndinachokera kwa Mulungu, ndipo ndikubwerera kwa Mulungu, kuti ndibwerere mu mawonekedwe a Mzimu Woyera."

261 Ndipo apa Iye ali, ndi ife lero, zithunzi za sayansi zojambulidwa za Ilo. Apa Iye ali, kuti adzatsimikizire kuposa chithunzi chirichonse chasayansi, chirichonse. Iye ali pano, kuti adzatsimikizire izo, pakuti Ilo ndi Iye. "Ine Mwana wa munthu

ndidzawululidwa mu tsiku lino." Tsopano, ndi Uyo *apo*. Ine ndikuyang'ana kumene pa Ilo.

262 Inu mukuti, "Kodi inu mukuliwona Ilo?" Yohane analiwona Ilo, nayenso, koma ena onsewo sanaliwone.

263 Penyani, kuti mutsimikizire izo tsopano. Mkazi ameneyo ndi mlendo kwa ine. Ine sindinamuwonepo iye—iye, mmoyo wanga. Koma iye ali ndi chinachake cholakwika ndi umodzi wa miyendo yake umene iye akuwupempherera. Ndi . . . Uko nkulondola, dona. Inu munali ndi opareshoni pa iwo. Amenewo ndi amuna anu akhala pafupi ndi inu. Inu simukuchokera kuno. Ndinu ochokera ku California. Dzina lanu ndi Roland. Vuto lanu la mmimba latha, nanunso, bwana. Inu munali ndi vuto la mmimba. Sichoncho inu? Chabwino, zonse zapita. Mwendo wanu wachira.

"Mu tsiku limenelo Mwana wa munthu . . . "

264 Apa, wakhala kumbuyo kudutsa *apa*, pali mwamuna. Iye ndi mwamuna wachikuda, chinachake chavuta maso ake. Iye ndi . . . Inde. Iye, ntchito imene iye amachita, iye amachita chinachake chokhudza galimoto, amapolisha magalimoto, wopukuta magalimoto. Kulondola. Maso anu akuyipira. Inu mwangokhulupirira kumene, sichoncho inu? Chinthu chinachake chachirendo chenicheni chinachitika kwa inu. Dzina lanu loyamba ndi Fred. Uko nkulondola. Dzina lanu lomaliza ndi Conn. Uko nkulondola. Inu mukukhulupirira tsopano? Maso anu sadzakuvutitsaninso pamenepo. Ine sindinamuwonepo bamboyo mmoyo wanga.

265 Bambo kuseri komwe uko, iye si wochokera kuno, nayenso. Akuchokera ku California. Ali ndi nsana woyipa, Bambo Owens. Ndi inuyo. Ambuye Yesu akuchizeni inu. Ine sindinamuwonepo bamboyo, mmoyo wanga, sindikudziwa kanthu za iye. Ine ndikungotsatira Kuwala kumeneko pamene Iko kukupita.

266 "Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira."

267 Mnyamata wamng'ono wakhala apa, ali ndi chophuka, wavala magalasi ndi suti yotuwa. Fred, Mulungu akuchiza iwe ngati ukhulupirire izo. Kodi iwe uvomereza izo? Chabwino. Ine sindinamuwonepo iye, mmoyo wanga.

268 Akazi a Holden, mwakhala apo kuchokera kwa iye, mukuvutika ndi vuto la diso. Ine sindikumudziwa mkaziyo, sindinamuwonepo iye mmoyo wanga, koma izo nzoona. Mukuona? "Ngati inu mungakhulupirire."

269 Mukulira chiyani, mlongo? Inu muli ndi kusokonezeka kwa manjenje, mphumu, vuto la mtima. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Mwakhala mutakhala kumapeto a mpando pamenepo. Ngati inu mukhulupirira, ndi mtima wanu wonse, Yesu Khristu akuchizani inu. Manjenje onsewo

achoka kwa inu, inu mukumverera ngati mwabwerera mu chikhalidwe chanu choyenera. Mdierekezi akukunamizani inu. Inu mukuvomereza zimenezo? Tsopano kwezani mmwamba dzanja lanu, nenani, "Ine ndikuvomereza zimenezo, ndiye." Chabwino. Izo zonse zatha.

270 Chiyani? Mpingo uwu ukudutsa mu ululu wa kubala. Kodi inu simupanga kusankha kwanu tsopano mu Kukhalapo Kwake? Ine ndakuwonetsani inu ndendende Mawu, chimene Iye anati Iye akanadzachita.

271 Kudutsa mnyumba muno, mfuseni aliyense amene anayamba wakhudzidwapo, kapena kuyankhulidwapo, kapena chirichonse chimene chinali, ndipo muone ngati ine ndinayamba ndawawonapo iwo, kuwadziwa iwo, kapena chirichonse cha iwo. Inu mukuganiza kuti munthu angakhoze kuchita zimenezo? Izo nzosatheka kwathunthu kuti izo zichitike.

272 Chabwino, ndi chiyani Icho? Mwana wa munthu. "Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ozindikira za mzimu, zinsinsi za mmitima." Ndendende basi monga Izo zinali pamene Iwo anasandulika thupi kuno pa dziko lapansi, mwa Mwana wa Mulungu, tsopano Izo zikuwululidwa ndi Mwana wa Mulungu pamene Iye wabwera kuti adzamuitane Mkwatibwi kuti atuluke mu kachitidwe kameneko. "Tulukani mwa izo. Khalani olekanitsidwa, atero Mulungu. Musakhudze zinthu zawo zodetsedwa, ndipo Mulungu adzakulandirani inu."

273 Kodi mwakonzeka kuti mupereke moyo wanu wonse kwa Mulungu? Ngati inu muli, imirirani pa mapazi anu, nenani, "Ine nditero, mwa chisomo cha Mulungu, ndilandira Iwo pakali pano, pa chirichonse chimene chiri mwa ine."

274 Aleluya! Matamando akhale kwa Mulungu! Inu mukumukhulupirira Iye? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndiye mungokweza manja anu ndipo mupemphere ndi ine.

275 Vomerezani zolakwitsa zanu. Ululu wa kubala! Ndi zovuta kufa, koma ifani pakali pano. Ifani, tulukani mu kusakhulupirira kwanu komwe. Tulukani kuchokera mwa iko. Awa ndi Mawu a Mulungu akuwonetseredwa, basi monga momwe Iwo anali pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi. Ndi Yesu Khristu kachiwiri pakati panu, wotsimikiziridwa.

276 Abrahamu analandira mwana nthawi yomweyo, mwana wolonjezedwa, izo zitachitika.

277 Ndipo Yesu akubweranso. Umenewo ndi Mzimu Wake. Iye ali pafupi kwambiri ku dziko lapansi, pafupi kwambiri kuti abwere, mwakuti Iye ndi wokonzeka kuti akulandireni inu, ngati inu mwakonzeka kumulandira Iye.

Tsopano kwezani mmwamba manja anu ndipo mupemphere ndi ine.

278 Ambuye Mulungu, mulole ansembe onse agwire maguwa. Mulole anthu alire. Mulole Lawi la Moto ndi Lawi la Mtambo zisunthire mwa anthu lero ndi kuwapangitsa iwo kudekha, Ambuye, kufika pozindikira Kukhalapo kwa Mulungu wamoyo ndi wamphamvu. Perekani izi, Ambuye. Alandireni iwo. Ine ndikupempherera pemphero ili kwa aliyense wa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu.

279 Mudzadzeni aliyense ndi Mzimu Woyera, amene alibe Mzimu Woyera. Ambuye, mulole chitsitsimutso cha msonkhano wokopa uno, msonkhano uno, chifalikire pakali pano ku kutsanulira kwakukulu, kwamphamvu kwa Mzimu Woyera. Mulole odwala achiritsidwe, akhungu awone, olumala ayende. Mulole kuwonetseredwa kwa Mulungu wamoyo kubweretsedwe pamaso pa anthuwa, monga zakhala zikukhalira madzulo ano, ndipo mulole anthu alandire izo. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupempha izi.

280 Kwezani manja anu tsopano ndipo mumpatse Iye matamando, ndi kulandira chimene inu munachipempha.

65-0124 Ululu Wa Kubala
Ramada Inn
Phoenix, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org